


MAFUNSO NDI MAYANKHO

 Wina ananena mu Chipangano Chakale, “Ine ndinali wokondwa pamene iwo anati kwa ine, “Tiyeni tipite ku nyumba ya Ambuye.””

¹ Ndipo tsopano, indedi ndi usiku wotentha. Ndipo kwa inu alendo omwe muli ndi ife, inu mukhoza kuwona chifukwa chomwe ku Indiana kuli kovuta kukhalako mozungulira kuno—dambo ili. Ine ndikukuuzani inu, ndi 93° yokha apo, 93°. Kotero inu mukuona, pamene inu mufika mpaka chamma 120° monga kuliri ku Louisiana ndi Arizona, inu mukhoza kuzindikira chomwe ziri ndiye, momwe inu mumaloweramo kwenikweni. Ngati i—izo zikanakhala kuno, ife tikangowonongeka, izo zikanakhala zonse. Koma ndi bwino kukhala tiri kuno kudzaika mu nthawi ino ya kupembeda.

² Nditapita kwathu mmawa uwu, ine ndinangomverera bwino, kwenikweni za... Ine ndikukhulupirira kuti ambiri anachiritsidwa mmawa uwu oti—omwe sakuzindikira izo, mwinamwake, mpaka nthawi ino, koma iwo akhala bwino; chifukwa Mawu a Ambuye anali ofunikira mmawa uwu kwa mitima yathu.

³ Ine ndinali basi... Pamene ine ndinayamba kuti ndizichoka, izo zimawoneka ngati makoma awa anali pafupi kupuma ndi—amakhala ngati akupopedwa ndi Mzimu Woyera chomwecho mkati muno. Ndipo ine ndinali wokondwa kwambiri chifukwa cha izo.

⁴ Ine ndinali kumumvera M’bale Smith, bwenzi wanga, akupemphera mphindi pang’ono pokha zapitazo, mbusa wa Mpingo wa Mulungu, Anderson. Ndipo M’bale Smith ali ndi katraki kakang’ono, ine sindikuganiza kuti ife tinawagawa iwo kuno ku Kachisi. Ngati aliyense wa inu mulibe katraki kakang’ono ako, inu mukakawerenge iko. Ako ndi katraki kakang’ono kododometsa; izo ndi mwamtheradi Choonadi Chamwamalemba. Ndipo ine ndinatengera ochuluka a iwo ku Chicago ndi malo osiyana kuti ndikawagawe iwo, chifukwa iwo ndi traki yachoonadi kwenikweni, yodabwitsa. Ndipo ine ndikudziwa kuti iwo analembedwa kuchokera mu mtima womwe uli wodzipereka ndi womukonda Mulungu. Popanda cholinga chodzikonda paseri pake M’bale Smith, basi yense Mkhristu. Chotero ife tiri okondwa kukhala tikuyanjana usikuuno ndi anthu a chikhalidwe choterocho.

⁵ Ine ndikukhulupirira ine ndikumuwona mzanga wabwino, M’bale Borders pano o—ochokera uko ku California. Ndipo iye a—anandichitira ine ntchito yaikulu posakhalitsapa—kwa Ambuye—uko mu—uko—kuyambira ku msonkhano waku San

Jose limodzi. Ine ndikuyembekeza inu mudzachita ntchito yabwinonso pa wina ukubwerawu M'bale Borders. Ndipo ine ndimamukonda M'bale Borders, chifukwa ine ndapeza mwa iye mzimu wofatsa, waulemu. Ndipo i—ine ndikuganiza uwo ndi mtengo waukulu. Ine ndikuganiza munthu yemwe ali ndi mzimu wa mtundu umenewo ayenera kumakhala wokondwa kwambiri.

⁶ Alipo ochuluka kwambiri ena muno, omwe ine sindingakhoze basi kuwawerengera omwe iwo ali. Ine ndikumuwona M'bale Collins kumbuyo uko, m'bale wathu, n—ndi atumiki ena, ndipo bwenzi lathu labwino M'bale Sothmann, banja lake, ochokera Kumpoto kwa Saskatchewan. Ndipo ine ndikumudziwa M'bale Evans ali muno; ine sindinamuwone iye panobe, koma ine ndaliwona banja lake, o—ochokera uko k—ku Georgia. Ndipo pali M'bale Palmer apo o—ochokera uko ku Georgia, n—ndi M'bale West, ine ndikukhulupirira, ochokera ku Alabama kapena Georgia. Kodi inu mukuchokera kuti M'bale West? I. . . Ndi. . . O, Huntsville. Ndiyeno. . . O, tinali okondwa basi kukuwonani nonse inu mkati muno.

⁷ Ndipo tsopano, M'bale Lyle, kumbuyo uko, Wood, ochokera—uko kumpoto kwa Indiana, ndi okondedwa awo. Ndipo ine ndikuganiza M'bale Charlie ali pano, mzanga wakale—mzanga wosaka naye wochokera uko ku Kentucky (wosaka bwino agologolo wachiwiri mu Kentucky, wosaka bwino agololo wachiwiri. Iye andilipiritsa ine pa izo. Chabwino!) ndi mkazi wake ndi banja. Ndi kwa nonse inu, moni wa Chikhristu.

⁸ M'bale wamng'ono pano, ine sindingakhoze kulingalira dzina lake—pano, osiyana onse. Koma inu nonse mukudziwa kuti ine ndithudi ndikukuyamikirani inu potuluka usikuuno kudzapembedza nafe pa kachisiyu.

⁹ Ndipo tsopano, usikuuno ndi usiku wosazolowereka pa kachisiyu, chifukwa ndi usiku wa funso ndi yankho. Ndipo izo kawirikawiri zimabwera pafupi kamodzi chaka chirichonse kapena pa ziwiri. Ndipo chifukwa chomwe ine ndimachitira izo, ndi kuti ndizikumbukira zomwe ziri mmalingaliro a anthu, chotero kuti ine ndizidziwa basi lomwe funso lawo liri. Kumulola aliyense kuponyera funso umu, ndiyeno nkuliyankha ilo kuchokera pa nsanjapa.

¹⁰ Tsopano, mu izi ine sindinapeze—ine ndimaganiza kuti izo zikanakhala zolimba kwambiri, koma ine ndangokhala ndi mafunso apang'ono kwambiri. Chotero izo sizititengera ife motalika kuti tiwayankhe iwo. Ine ndinali kuganiza kuti ndipeza odzaza lichero lonse, koma ndi apang'ono okha ndi ophweka kwambiri. Koma ena a iwo ndi okhudza chiphunzitso.

¹¹ Ndipo mu chiphunzitso ichi ine ndisowa kuti ndiyankhe funso la anthu mosadziwa omwe iwo anali (chifukwa ambiri sanaike maina awo pa mafunsowo); ndipo chotero, ine ndikhala ndikuwayankha iwo molingana ndi chiphunzitso chomwe ife

timachiimira pa kachisiyu. Ndipo pochita izo. . .Ndipo ngati zichitika kuti zikukhala ngati zikugunda waya pang'ono pa abale athu ena odzacheza kapena alongo, ife sitikanakhala titachita dala izo. Ife sitimakhulupirira kuti aliyense azikangana pa nsonga zazing'ono za Mwamalemba. Ife timakhulupirira kuti Khristu anafa kuti adzatipulumutse ife tonse, ndipo ndife tonse opulumutsidwa kupyolera mu Magazi Ake.

¹² Koma monga mpingo ndi monga a—anthu, osonkhana, ife tiyenera kukhala ndi chiphunzitso chomwe ife tikuchiimira polinga kuti tikhale m—mpingo. Ndipo chiphunzitso ichi chomwe ife tikuchiimira, ndi kukhoza kwa kudziwa kwathu ku Mawu a Mulungu, Choonadi cha Mulungu. Tsopano, inu muli nawo ufulu wangwiro kuti mukayang'ane pa izo mwanjira yosiyana ngati inu mukufuna kutero. Ndipo chotero, ngati I . .

¹³ Winawake akufunsa mafunso apa . . . Angapo a iwo maka ndi ozama. Ndipo ine ndiwayankha tsopano mwakukhoza komwe ine ndikudziwira basi.

¹⁴ Tsopano, umu momwe ine ndikuyesera kuti ndichitire nalo funso. Funso . . . Ngati—munthu angatenge Lemba limodzi lokha ndipo akhoza kulipangitsa Ilo kunena chirichonse chimene inu mukufuna kuti Ilo linene. Koma Lemba, Lemba lirilonse ndi Choonadi. Ndipo Ilo ndi langwiro kwambiri, mpaka Mulungu wopandamalire Yemwe analiyankhula Lembalo, Ilo ndi langwiro kwambiri mwakuti Ilo liribe konse mathero. Chotero ndiye, Ilo liyenda kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso, chinthu chomwecho. Izo sizidzasiyana konse. Ndiyeno, ngati Baibulo liri Mawu owuziridwa a Mulungu, Ilo silingadzisemphanitse Lokha pamalo ena. Ilo lipita njira yonse kudutsa mu Lemba.

¹⁵ Tsopano, nthawi zambiri. . .Monga ine ndinali ngati wamwano pang'ono mmawawu pa kulalikirira Samusoni ndi Delila ndi mpingo mwa chidziko, koma ine sindimatanthauza kuti ndikhale wamwano, koma ine ndikutanthauza kuti ndikhale woonamtima, woonamtima basi monga ine—kukhudzidwa kwanga kuli.

¹⁶ Tsopano, mu Malemba, Iwo pokhala Mawu osalephera a Mulungu, ine ndikukhulupirira kuti pali chinthu chimodzi chokha chomwe chingakhoze kutanthauzira molondola Lemba, icho ndi, Mzimu Woyera. Ine ndikukhulupirira ndiwo . . .Ndipo Mzimu Woyera Yemwe analemba Malembawa, ndipo anati Iwo ndi opanda kumasulira kwa mseri. . .Chotero, ngati iwo angayende njira yonse kudutsa mu Malemba, Iwo uyenera kukhala uli Mzimu Woyera womwewo ndiye, njira yonse kudutsamo, kuti uwatanthauzire Iwo.

¹⁷ Koma tsopano, anthu ambiri mu mipingo yawo ndi zikhulupiriro zawo, ali nazo zosiyana, kenakake kakang'ono komwe iwo amagwirirako komwe kangakhale kali kosiyana

pang'ono pokha. Ngati iwo ali, muzingochita izo monga momwe ine ndimachitira pamene ine ndikudya chitumbuwa cha nthuza. Ine sindimadya konse njereyo. Pamene ine ndiluma njere, ine ndimangoitayira njereyo kwina ndi kumapitiriza kudya chitumbuwacho. Chotero izo nzomwe inu muzichita.

¹⁸ Ine ndikumuwona Mlongo wathu Wooten ali ndi mwana wawo wamng'ono ataima apo. Ngati iye watenthedwa, Mlongo, ndipo inu mulibe pokhala, ine ndikudabwa ngati mmodzi wa abale athu sangatenge mpando kuchokera mkatimu ndi kukaukhazika iwo kumbuyo uko pafupi ndi chokupizira mphepo kuti Mlongoyu akhoze kukhala ndi malo ozizirirapo kuti akhale pansu. Ife tingakhale okondwa kuti tichite zimenezo, ine ndikutsimikiza, aliyense wa abale awa. . . Chokupizira mphepo kumbuyo uko, Mlongo, kulondola—chikukupizira mbali iyi ndipo apo pali mpando. Ngati inu mukufuna kuti muugwiritse ntchito iwo, inu mungopitirira nazo ndithu.

¹⁹ Tsopano, aliyense wa inu abale yemwe mukufuna kuti muvule chikhoto chanu, ingopitirirani nazo kumene, dzipangeni nokha kumverera bwino ndi wokondwa.

²⁰ Tsopano, ine ndikuti ndilifunse thupili, kuti ngati iwo ati andipempherere ine. Sabata yotsatira iyi ine ndiyenera kuti ndipite ku California, njira yonse mpaka uko, ku msonkhano wa usiku umodzi. Usiku umodzi wokha kukalalikira ku Msonkhano waukulu wa Amuna Amalonda Achikristu Akulikonse. Koma iwo awulengeza iwo, ndipo ife tikuyembekeza zikwi zambiri za anthu kuti akakhala uko. Ndipo ine sindikanafuna kuti ndiwakhumudwitse iwo. Ndipo ine ndinawauza iwo kuti ine ndikanabwera ngati ine ndikanati ndisakakhale ndiri ku Australia pa nthawi iyi, chomwe ine ndinakonza kuti ndikakhale ndiriko. Chotero zitipemphererani ife.

²¹ Ndipo aliyense wa inu amwendamnjira okondedwa apa dziko lapansi lino omwe muli pa tchuthi chanu ku ntchito zanu za pa tsiku ndipo mukanafuna kuti mudzakhale mu umodzi wa misonkhano, kudzakakhala kuli utumiki wa masiku atatu ku Cleveland, Tennessee, Mpingo wa Mulungu. Ine ndikuganiza uwo ndi Mpingo wa Pentecostal of God, kuchita kwa Tomlinson. M'bale Littlefield, David Littlefield, ndi m'busa, njonda yabwino kwambiri ya Chikristu. Iyeyo ndi wa Chiyaukee wochokera Kumpoto, wochokera ku Bangor, Maine, koma Mkristu weniweni, m'bale wabwino.

²² Ndipo chotero, ngati inu muli pa ulendo wanu ndipo mukufuna kuti mutabwerako, mwinamwake Lolemba usiku kudzakhala kudalitsa kwa kachisi wamkulu kwambiri yemwe iwo amumanga. Ndiyeno, Lachiwiri ndi Lachitatu usiku wa sabata yamawa, Ambuye akalola—osati sabata ikubwera iyi, sabata yotsatira—kudzakhala kuli utumiki wa machiritso, yomwe iti idzakhale pa 6, pa 7, ndi pa 8.

Tsopano, ife tisanatsegule Mawu, ine ndikanafuna ngati tikanaweramitsa mitu yathu mphindi yokha kwa pemphero.

²³ Ambuye Mulungu, Atate wofunika wa ife tonse, Yemwe munamubweretsanso Ambuye Yesu kuchokera kwa akufa ndipo mwamupereka Iye kwa ife mwa mawonekedwe a Mzimu Woyera. Mutatha kupachikidwa, mutafa, mutaikidwa mmanda, mutauka pa tsiku lachitatu, ndipo munakwera ku ulemerero, komwe tsopano mukukhala pa dzanja lamanja la Ufumu mmwamba, nthawizonse wamoyo kuti muzikhalira pakati, Wansembe Wamkulu yemwe angakhoze kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu ndipo amadziwa ngakhale mpheta yaing'ono ng'ono yomwe ingagwere mu msewu, Iye angakhoze bwanji kungodutsa pa kumvera kwa ana Ake omwe akhala usikuuno mu nyumba ino yotentha kuti angomva Mawu. Ine ndikutsimikiza, Ambuye Mulungu, ngati ife tikanati tisafunse konse, kuti Inu mukadatsanulira madalitso Anu pa iwo chifukwa cha maimidwe awo olimba pa malo awo antchito usikuuno.

²⁴ Pali alendo pano, Ambuye; ife tikuwapempherera iwo ndi mipingo yawo. Pali atumiki odzozedwa a Uthenga—odzozedwa ndi Mulungu—akhala pomwe pano, omwe ali okwanira kwambiri kuti ayankhe mafunso awa kuposa ine. Ndipo ine ndikupemphera, Ambuye Mulungu, kuti Inu mulole Mzimu Woyera ubwere kwa ife usikuuno ndi kudzatipatsa ife zinthu zoyenera zoti tizine, zomwe zingabweretse chisangalalo chosayankhulika ndi chodzaza ulemerero kwa mitima yathu pomwe ife takhala palimodzi mu malo ammwambamwamba mwa Khristu Yesu, tikuphunzira Malemba mopanda kukondera, mopanda kumverera koipa kulikonse, koma kungoti tidziwe chomwe chiri Choonadi ndi kumapembedza Choonadi. Perekani izi, Ambuye.

²⁵ Ife tikupempha kuti mumudalitse M'busa wathu wokonedwa, M'bale Neville, yemwe waima molimba pa malo a ntchito chaka ndi chaka kudutsa motentha ndi mozizira kuchita ubusa ndi kulisya nkhoa za gulu lomwe limasonkhana pano. Tikupemphera kuti Mzimu Wanu ukhale pa iye, muthandizeni iye. Ndipo muwadalitse onse omwe alumikizana ndi kachisi. Ndipo posachedwa, Ambuye, ngati icho chiri chikhala chifuniro Chanu, ife tikuyembekezera kachisi wokonedwa, wamkulu kudzaima pangodya pano pomwe ife tingadzakhale ndi sukulu, yomwe tingamadzawaphunzitsiremo atumiki aang'ono ndi kumawatumiza iwo ku ngodya zinai za dziko lapansi kuti akalimbanire mooni chikhulupiro chomwe chinaperekedwa kamodzi kwa oyera.

²⁶ Ambuye, ife tikukalamba, inemwini, ndipo posachedwa ine ndiyenera kuti ndidzapereke Baibulo mmbuyo mmanja a winawake. Tithandizeni ife, Ambuye, mu kuyesetsa uku. Muyankhe mafunso athu usikuuno mwa Mzimu Woyera, pamene

ife tikudalira mwa Iye, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu Mwana Wanu. Amenii.

²⁷ Tsopano, ine ndikudziwa kwatentha kwambiri, koma ine sindimakonda kulambalala funso mpaka ine nditaganiza kuti ndachita molungama pamaso pa Mulungu pakuliyankha ilo. Tsopano, ife tiribe ochuluka ambiri; ine sindinawawerenge iwo, ndi basi—apang’ono kwambiri. Koma izo zikhoza kukhala kuti ife tikhoza kusafika kwa onse a iwo, koma ife tikufuna kutero ngati nkotheke. Ndikuti ndimufunse msungwana wamng’ono uyu wavala za pinki wakhala apayu. . . Tabwera kuno, Wokonedwa. Ine ndikukhulupirira kuti uyo ndi msungwana wamng’ono wa M’bale Beeler. Ine ndikufuna kuti iwe utenge mafunso awa pansi apo ndipo ungowasakaniza iwo, iwe ukudziwa chomwe ine ndikutanthauza, kungowasakaniza pa lina limzake, monga chonchi, inu mukudziwa, chotero—ndiye muwabweresenso iwo kwa ine. Mwaona? Kuti ine ndisasakanize mafunso a munthu aliyense, inu mukudziwa, kumaganiza kuti ine ndinangoyankha limodzi, ndipo ine ndisanafike kwa linalo; ine sindikanafuna izo. Ingomulolani msungwana wamng’ono yawasakanize iwo pamodzi, ndiyeno ife tingotenga iwo omwe ali pamwamba pake ndi kuwayankha iwo pamene ife tizibwera nazo.

²⁸ Tsopano, ngati pangakhale pali (zikomo iwe, Wokomantima)—ngati pangapezeke kuti pali funso mu malingaliro a winawake, ine ndikufuna kunena, kuti ine ndikanakhala wokondwa ngati nditatsiriza kuyankha funso lanu ndipo zikapanda kuwoneka kuti mwakhutitsidwa, ndiye mungokweza dzanja lanu nkuyankha. Pakuti inenso ndiri nalo pano Lachigriki, Lachihebri—zonse Chigriki ndi Chihebri mu lexicon yapachiyambi, kuti ndizipeza kulongosola kwa mawu (inu mukuona?), chifukwa ena a iwo akufunsa mawu—Chihebri ndi Chigriki aponso.

²⁹ Ndipo tsopano, Ambuye atithandize ife pamene ife tikuyankha. Ndipo ndiloleni ine ndifotokoze izo momveka. . . (Kodi mukukhoza kundimva bwino ine kumbuyoko, kwezani mmwamba manja anu ngati inu mungathe. Ndizo zabwino.) Ndirole ine ndifotokoze momveka tsopano, kuti pa kuyankha mafunso awa, siziri mwa kukondera kulikonse, koma aliyense akumbukire kuti mu kachisi ngati zibwera mwa chiphunzitso, ife timayenera kuti tiyankhe izo molingana ndi kukhudzidwa kwathu pano, osati kuti tisokoneze malingaliro anu, koma k—kuti tibweretse kukhudzidwa kwathu. Ndipo nthawizina ife timazikhomerera izo mothina zedi. Koteru muzikumbukira, ndi kungoti tizipange izo motsimikizika kwa opembedza.

75. Tsopano, loyamba lake pamwambapo. O, inde, ili ndi funso laling’ono. Ilo si funso, ndi. . . Chabwino, ilo ndi funso. **Ndi winawake yemwe akufuna kuyankhulana kwa mseri ndi ine koyambirira kwa sabatali.**

³⁰ Tsopano, kuyankhulana kwapadera uko, ine ndikuuzani inu momwe ife timachitira izo. Izo zinali mwa kuti ife timangokhala ndi kuwagwira *mwachisawawa, ndani atayambe, uyu, uyo*, koma ife tirino ndi kachitidwe kwa izo. Ndipo chotero, pali anthu ambiri omwe amabwera mu mizere ya pemphero, omwe akhoza mwinamwake kudutsa mu mzere wofulumira, kapena ali ndi cholinga chomwe sakudziwa zomwe angachite nazo, ndiyeno, iwo amafuna kuti amve kuchokera kwa Ambuye. Tsopano, iwo ali nawo ufulu wangwiro kwa izo; ndi chomwe mphatso yauneneri iyi inaperekedwera, ndi kwa chimenecho, cholinga icho chokha.

³¹ Mu Baibulo ngati iwo ankafuna kuti adziwe chirichonse, iwo ankapita uko kwa aneneri, ndipo iwo ankapemphera ndi kuimba nyimbo mpaka Mulungu ankayankha. Bwanji, Iye si Mulungu yemwe angadyetse gulu lina ndi kulipha gulu linalo ndi njala. Iyeyo ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndipo chotero, nchomwe chiri cha Iwo.

³² Pa zoyankhulana zapadera izi, pamene ife titenga vuto, ine sindimalisiya ilo mpaka ine nditamva kuchokera kwa Mulungu mwanjira ina kapena imzake. Izo zimabwera mwapang'ono pang'ono. Ngati izo zitenga miyezi sikisi kapena chaka, ife timangokhala ndi icho mpaka ife titakhala ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuona? Ndipo chotero, izo zimabwera mwapang'ono pang'ono, ndipo pali zikwi akuitana. Koma ife . . .

³³ Tsiku lina ine ndinali ndi bambo mmenemo—ine ndikukhulupirira izo zikanakhala miyezi pambuyo pa miyezi chiyambireni pomwe bambo uyu anali akufuna ubatizo wa Mzimu Woyera, wa Chibaptisti. Koma ife sitikanati timumasule iye, tinangomulola iye kuti azibwera, ndipo potsiriza mwa chisomo cha Mulungu pa zoyankhulana zapadera. . . Atangolowa umo—iye nthawizonse ankafuna kuti aziwona masomphenya lomwe linali vuto—ndipo masomphenya anamukhudza, ndipo iye analandira Mzimu Woyera atakhala mu mpando wake womwewo.

³⁴ Ndiye—Mkatolika, wotembenuzidwa mwatsopano, anabwera uko kuchokera ku Chicago tsiku lina yemwe wakhala pa zoyankhulana zapadera—akuyesera kuti alowe umo—kwa pafupi zaka ziwiri; koma pa kuyankhulana naye koyamba, maminiti fifitini mu chipinda, Ambuye anawonetsa masomphenya, chifukwa ndi zonse, anawulula chinthu chonsecho, zomwe iye ankayenera kuti achite iye asanawulandire Mzimu Woyera. Mwaona, ndizo zomwe izo zimachita.

³⁵ Tsopano, ngati aliyense pa nthawi iliyonse. . . Pamene kuitana kubwera umo ndipo iwo akufuna kuti awone kapena kukhala ndi kuyankhulana uko, ngati iwo angaitane, Butler 2-1519, ofesi ikhoza kukutumizani inu ndendende

basi pomwe kuyankhulanako kungadzakhalepo. Ndiyeno, muzinena kuti kuyankhulana kwanuko ndi kwa chiani, kuti iwo adziwe kuti ndi nthawi yochulukuka bwanji yoti angaikire izo. Ndiye izo zimalungamitsa izo, ndi munthu aliyense... Ndiye ngati kuchulukuka kwa nthawi iyo sikukukwanira, ndiye ife timabwereranso ku vuto limenelo kachiwiri. Izo zimaikidwa pa kaundula pomwe, ndipo ife timazisunga izo mpaka ife titamva kuchokera kwa Mulungu mwa masomphenya kapena njira yina yomwe Mulungu angayankhulire. Kotero umu ndi momwe zoyankhulana zathu zimasungidwira.

³⁶ Chotero, onani, pamene ine ndituluka, anthu amaganiza nthawizina. “M’bale Branham, inu simumawawona anthu mokwanira.” Iwe sungakhoze kuwawona anthu ndi kukhala ndi Mulungu pa nthawi yomweyo. Mwaona? Ine ndimakhala ndi winawake poonekera, ndipo i—ine ndiri ku mphanga kapena kwinakwake ndikupemphera, ndi—ndi... .

³⁷ Ine ndikufuna kuti ndiwone chomwe ichi chikunena. [M’bale Branham akuwerenga cholembedwa kwa iyemwini—Mkonzi.] O, inde. Inde, inde uyu anali mwamuna (Gene anangochiika icho apa) kuti... Mwamuna anabwera kuno kuchokera ku Chicago tsiku lina, yemwe adotolo ankafuna kuti awucheke mtima mwakemo, ndi kuwudula iwo mowutsegula kuti awone chomwe chinali vuto mkatimo. Ndipo Mzimu Woyera unaulula ndendende basi chomwe chinali, ndipo iye sanasowe kuti achekedwe motsegula; iye anachizidwa. Chotero inu mukuona, izo zimatanthauza zochulukuka. Ndipo kuti ndikusonyezeni inu momwe izo zimabwerera mochedwa, ine ndinadikirira mwiniwanga yankho lochokera kwa Mulungu, kwa masomphenya, kwa zaka fifitini. Mulungu... . Ndiyeno wina anabwera ndipo sanachite kudikirira maminiti atatu. Mwaona? Ndi basi... Mulungu amayankha mu nthawi Yake yake. Ife sitimawulamulira Iwo, Iwo umatilamulira ife.

76. Tsopano, funso lachiwiri lomwe liri pamwamba ndilo...
M’bale Bill, kodi Ambuye angagwire ntchito mwamphamvu kupyolera mwa ine mu gulu lomwe samakhulupirira mu mphatso zauzimu?

³⁸ Palibe dzina pa ilo, koma munthuyu akufuna kuti adziwe ngati Ambuye angakhoze kugwira ntchito ndi iwo pamene iwo akugwira ntchito mu gulu lomwe silimakhulupirira mphatso zauzimu. Ine ndikuzikaikira izo mochulukuka kwambiri.

³⁹ Ine ndikukaikira kwambiri, mzanga wokonedwa, kuti Ambuye angagwire ntchito mokwanira kupyolera mwa inu, chifukwa inu mwalumikizidwa nao pakati pa osakhulupirira, ndipo Baibulo linati, “Musadzimange goli nokha ndi osakhulupirira, koma mutuluke pakati pa iwo, ndipo kukhala inu olekanitsidwa, atero Ambuye, ndiye ine ndidzakulandirani inu.” Ine ndikukhulupirira ngati inu mukukhala mu mzinda,

komwe kuli mpingo umene umakhulupirira mu zizindikiro ndi mphatso zauzimu, ndipo inu muli nazo zinthu izo zikugwira ntchito pa inu, ine ndikanati ndizipita ku mpingo uwo kumene iwo amakhulupirira izo.

⁴⁰ Ndiyeno ine ndikhoza kunena chinthu china, monga ine ndachitira—kawirikawiri kupereka—ndimafuna kuti ndipereke Lembu. Inu mwinamwake, mzanga wokondedwa, mwayesera mwakukhoza kwanu konse kuyesera kuti muwabweretse anthu awa pokhulupirira, kuyesera kuwapangitsa iwo kuti akhulupirire, ndipo iwo basi sakukhoza kuchita izo, mwinamwake. Ndiye ine ndikuti ndikupatseni inu Lembu lomwe ine ndikukhulupirira kuti Ambuye Yesu akanakondwera kuti ife talipereka.

⁴¹ Ngati inu mwayesera, ngati inu mwayankhula nawo abusa, ngati inu mwayankhula kwa osiyanasiyana ndipo iwo akunyalanyaza izo kwathunthu ndipo sakuzikhulupirira izo, pano pali zomwe Yesu ananena mu Mateyu 7:6 zokhudza oterowo.

Musapereke icho chomwe chiri chopatulika kwa agaru, ngakhale kuponyera. . . ngale zanu pamaso pa nkhumba, kuwopa kuti zingapondereze izo kumapazi awo, ndi kupotoloka. . . ndi kukung'ambani inu.

⁴² Kotero ine sindimakhulupirira kuti ine ndingamagwirizane ndi gulu lomwe silimakhulupirira mu Uthenga wathunthu wa Ambuye Yesu Khristu, kukhulupirira kuti Iye anali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Pamene ine ndikhala mu gulu ndi kumuwona Iye akugwira ntchito ndi kumachita basi monga Iye anati akanamadzachita, ine ndikukhulupirira ine ndikanamverera ndendende—wolungamitsidwa powauza anthu kuti atuluke pakati pa oterowo ndi kudzipezera nokha—mpingo wabwino womwe umalalikira Malemba onse ndi kuwakhulupirira Iwo.

77. Tsopano, funso lotsatira ndilo: Kodi ndi zoonza kuti iwe sumapulumsidwa kupatula ngati walandira Mzimu Woyera?

⁴³ Apo ndikhoza kutenga pafupi maora asanu abwino okambirana pa izo. Pamene inu mumuvomereza Khristu ngati Mpulumutsi wanu ndipo mulino wokonzekera ubatizo mu madzi, inu simunatembenuke apabe; inu mwangokhulupirira kuloza ku kulapa. *Kutembenuka* kumatanthauza “kukhala utasinthidwa.”

⁴⁴ Tsopano, kuti tizipange izi moyenera, Yesu anati kwa Petro yemwe anali atamutsatiranso Iye kwa zaka zitanu ndi theka. . . Ndipo mu Bukhu la Mateyu mutu wa 10 Yesu anamupatsa Petro mphamvu yotsutsa mizimu yosayera, kuti apite ndi kumakazitulutsa izo, kumakachiza odwala, ndi kumakalalikira Uthenga. Iye anali nazo mphamvu zochitira

izi. Ndipo mu Yohane Woyera 17:17 Yesu anamuyeretsa Petro kudzera mu Choonadi, anati Mawu anali Choonadi, ndipo Iye anali Mawu. Ndiyeno pa—isanafike Pentekoste Iye anati. “Iwe ukadzatembenuka kaye, ndiye uzidzawalimbikitsa abale ako.” Iwe ukungotenga masitepe opita ku kutembenuka pamene iwe ukukhulupirira ndi chomwe ukuchitapo.

⁴⁵ Tsopano, ine ndikudziwa ambiri a inu, amzanga Achibaptisti ndi Achipresbateria, mumatsutsana nazo izo, chifukwa inu mumabwerera ku Lemba ili... Tsopano, apa ndi pamene ine ndikuti ine ndiyenera kuti ndizikhomerere izo pansi. Mwaona? Inu mumabwerera ku Lemba: Abraham (Aroma 4) *anakhulupirira* Mulungu, ndipo izo *zinawerengedwera* kwa iye kapena *kunapatsidwa* kwa iye kuti ndi chilungamo. Abrahamu *anakhulupirira* Mulungu, ndipo Mulungu anawerengera kwa iye ngati chirungamo pa maziko a chikhulupiriro chake pakukhulupirira. Koma kuti atsimikizire kwa Abrahamu, Iye anamupatsa iye (kusawerengerako, kuti sanawerengedwere ku machimo ake, ndiye Iye anali—anamuika iye kuchoka ku machimo ake), chifukwa iye anakhulupirira, Iye anamupatsa iye chizindikiro. Ndipo chotero inu, amzanga okonedwa a Chipresbateria ndi Chibaptisti, mumalephera kuti muziwone izo. Mwaona? Iye anamupatsa iye chisindikizo cha mdulidwe ngati umboni, ngati chitsimikizo, kuti Iye wachilandira chikhulupiriro chake mwa Iye. Ndipo nchifukwa chake Paulo mu Machitidwe 19 ananena kwa abale Achibaptisti aja, omwe anali naye Apollo monga m’busa wawo, akukhulupirira Uthenga momwe Yohane anali atawulalikira Iwo, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni chanu?” Inu mukuona, iwo anali atakhulupirira koma anali asanatembenuke apabe.

⁴⁶ Tsopano, ife timatenga zolakwika—mu mawu a *kutembenuka* lero. Ife timanena kuti munthu yemwe watembenuka mtima ndi munthu yemwe wasiwa kumwa ndi chirichonse ndi kumapita ku mpingo, kapena kujowina mpingo. Iye akhoza kujowina mpingo, koma icho si chizindikiro kuti iye watembenuzidwa. Iye sanatembenuke mpaka moyo wake wakale utafa, ndipo iye atakwiridwa mwa Khristu, ndipo atawuka ndi Iye mu chiwukitsiro cha utsopano wa moyo, pamene Mzimu Woyera walenga mwa iye chiyembekezo chamoyo cha Moyo Wamuyaya chomwe chimabwera kokha kudzera mwa Mzimu Woyera. Mwaona?

⁴⁷ Tsopano, tsopano, ine ndimalidziwa Lemba lalikulu ilo, ine ndimaligwiritsa ntchito Ilo mwiniwanga—Ine ndiri nalo Ilo litalembedwa apa—Yohane Woyera mutu wa 5, ndime ya 24. Ilo ndi Lemba loliweta kwa ine. Pakuti Yesu ananena izi: “Indetu, indetu, ine ndinena kwa inu, ‘Iye amene akhulupirira pa Ine ali nawo Moyo Wamuyaya.’” Ndiroleni ine ndiziwerege izi, chotero kuti ine ndizitenge bwino Izo mwangwiwo. Yohane Woyera 5,

ndipo ine ndikufuna kuti inu mumvetsere mwacheru tsopano pamene ife tikulowa mu Lemba ili, 5 ndi ndime ya 24.

Indetu, indetu, ine ndinena kwa inu, Iye amene amva mawu anga, ndi kukhulupirira pa iye yemwe anandituma ine, ali nawo moyo wosatha, ndipo sadzabwera ku kuveruzidwa; koma wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku moyo.

48 “Iye amene akhulupirira pa Ine.” Tsopano, Lemba limanena kuti palibe munthu anganene kuti Yesu ndi Khristu mwa Mzimu Woyera mokha. Chotero inu simungakhoze kukhulupirira kuti Yesu ndi Khristu mpaka inu mutalandira ubatizo wa Mzimu Woyera. Inu mukungochitira umboni kapena kunena zomwe Lemba limanena, kunena zomwe abusa amanena, kunena zomwe amayi amanena, kapena mlaliki wina wabwino amanena. Koma inu simukuzidziwa izo inumwini mpaka Iye atachitira umboni chiwukitsiro Chake kwa inu. Ndipo palibe munthu angakhoze kumutcha Yesu kuti ndi Khristu mpaka ziri mwa Mzimu Woyera.

49 Chotero, funsolo ndi loti, kuti munthu amapulumsidwa, ine ndikukhulupirira, ngati iye akuyang’ana cha ku Kalvare, nafa mu chikhalidwe chimenecho. Ndithudi, ine ndikukhulupirira iye adzapulumutsidwa; ine ndikukhulupirira iye akanati adzadutse ngati iye analibe mwayi poyambapo. Koma zimatengera pa...Inu mumabwerera kwa mbala yokufa pa mtanda. Koma kumbukirani, uwo unali mwayi wake woyamba ndi wotsiriza. Inu muli nawo wina usikuuno. Musati mudikire mpaka nthawi imeneyo, chifukwa mwina sizingakhoze kudzakhala mwanjira imeneyo ndi inu. Inu mwina simungadzakhoze kudzakhala ndi kulapa kwa pa kama ya imfa. Ine ndikukuuzani inu, izo ndi zabwino, koma izo ndi za mwayi wochuluka kwambiri kuti utengerepo mwayi. Musati mudikire mpaka kama ya imfa; inu mulole iyi ikhale kama yanu ya imfa pakali pano, kuti inu muferepo tsopano ndi kukhala obadwa kachiwiri ndi Mzimu Woyera.

Tsopano, pa funso lotsatira ili...Tsopano, ngati pali funso pa izo ingokwezani dzanja lanu. Ine ndikhala wokondwa kuti ndichite mopambana kwambiri momwe ndingathere.

78. Kodi inu mungapapeze paliponse pomwe atumwi ankadya Mgonero itachitika Pentekoste? Kodi Paulo ankanthauza kuti anthu samawazindikira Mawu? Mzimu Woyera inali njira yokha yopembedzera Mulungu? Ngati iwe utenga vinyo ndi zotafunira, matenda ndi kugona zimabwera pa iwe?

50 Tsopano, apa pali mwinamwake malo pomwe ine ndikukhulupirira munthu wokondeka yemwe anafunsa izi mosakaika ali mozama ndi moonamtima pa izi, zomwe iwo akuzifunsazi, kapena iwo sakanati azifunse izi. Ndipo i—M’bale wanga kapena Mlongo, aliyense yemwe ali, ine ndiyankha izo

mwakuya basi ndi modzipereka monga inu mwayankhira izo—kapena mwafunsira izo.

⁵¹ Ine ndikufuna inu tsopano kuti mutembenezire ndi ine ku Bukhu la Machitidwe mutu wa 2, ndipo ndi—ife tiyambira ndi ndime ya 42. Mutu wa 2 wa Machitidwe, ndipo ife tiyambira, monga ine ndinanena, ndi ndime ya 42.

⁵² Tsopano kumbukirani, ine sindikukhulupirira kuti ine ndingapanene ndendende basi pamene Lemba likunena kuti Paulo anatenga Mgonero, ndipo Petro ndiye anafikira apo nawutenga iwo; koma pamene iwo akuyankhula za osonkhana, izo zinali mwa onse, aliyense. Ndipo ine sindikukhulupirira kuti Paulo akadalalikira chinachake ndi kuwauza ena kuti azichita, zomwe iye sakanati azichite. Chotero mu Machitidwe ife tikupeza izi:

Ndipo iwo anapitiriza mosasuntha mu chiphunzitso cha atumwi...chiyanjano,...(Penyani! Iwo anapitirira, mpingo wonse, thupi)...mopitirira mosasuntha mu chiphunzitso cha atumwi ndi mu chiyanjano,...(ndi, cholumikizira apo. Mwaona?)... ndi mu kunyema kwa mkate,...(Uwo ndi Mgonero)... ndi mumapemphero.

⁵³ Atumwi, omwe anali alaliki...Iwo anapitiriza mosasuntha mu chiphunzitso chawo, cha kunyema kwa mkate (Mgonero), ndi mu chiyanjano, ndi mumapemphero. Ndiye, ngati izo zikudulira kunja Mgonero kuuchotsa kwa atumwi, izo zikudulanso pemphero kulichotsa kwa atumwi. Mwaona? Tsopano, tiyeni tingowerenga mopitirira. Mwaona?

Ndipo mantha anadza pa moyo uliwonse: ndipo zodabwitsa zambiri ndi zizindikiro zinkachitidwa ndi atumwi.

Ndipo okhulupirira onse anali palimodzi, ndipo iwo anali nazo zinthu zonse mofanana;

Ndipo iwo anagulitsa zinthu zawo ndi katundu, ndipo anazipereka izo kwa munthu aliyense, momwe munthu aliyense analiri ndi chosowa.

Ndipo iwo, anapitiriza tsiku ndi tsiku mu mgwirizano umodzi mu kachisi... (Awo ndi atumwi ndi onse)... kumanyema mkate... (Mgonero nthawi iliyonse yomwe iwo anakomana)...

⁵⁴ Ichu chinali chiphunzitso cha atumwi ndi cha mpingo woyambirira, kuti nthawi iliyonse yomwe iwo ankabwera palimodzi iwo ankadya Mgonero. Nthawi iliyonse! Tsopano, ine ndikudziwa inu anthu Achikhristu omwe mumapita ku Mpingo wa Chikhristu (mpingo wa Chicampbell, monga ife timawudziwira iwo, ngati...Chifukwa pali iwiri ya iyo, wina ndi Mpingo wa Khristu, ndipo winawo Mpingo wa

Chicampbell.), inu mukuti, “Ife timaudya iwo mmawa wa Lamlungu lirilonse. Ife tiri nawo Malemba pa izo.” Inu muli ndi Lemba labwinoko pa izo kuposa Branham Tabernacle aliri. Branham Tabernacle amatenga iwo kamodzi pa mwezi. Koma Lemba liri, mowirikiza pamene inu mubwera palimodzi. Ndiko kulondola. Iyo ndi nthawi iliyonse.

Ndipo iwo, anapitirira tsiku ndi tsiku mu mgwirizano umodzi mu kachisi, . . . kunyema mkate nyumba ndi nyumba, ndipo ankadya chakudya chawo ndi kukondwa ndi umodzi wa mtima,

⁵⁵ Mwaona, nthawi iliyonse atumwi, akamakhala ndi misonkhano ya magulu a pemphero awa mu kachisi, nyumba ndi nyumba; nthawi iliyonse yomwe iwo anakomana, iwo ankanyema mkate, ankatenga Mgonero.

⁵⁶ Tsopano, Paulo, mu 1 Akorinto i—ife tikhozanso kuwerenga mutu wa 11, pomwe ife timapagwiritsa ntchito kuno pa Mgonero. . . Ine ndikhoza kuwerenga izo kuti izo zikhoze kukuthandizani inu, 1 Akorinto mutu wa 11. Mvetserani Paulo akuyankhula tsopano, ndime ya 23.

Pakuti ine ndinalandira kwa Ambuye izo zimenenso ine ndinazipereka kwa inu, Kuti Ambuye Yesu usiku womwewo . . . iye anaperekedwa anatenga mkate:

Ndipo pamene iye anayamika, iye anawunyema iwo, nati, Tengani, ndipo idyani: ili ndi thupi langa, lomwe lanyemedwera kwa inu: muzichita ichi pondikumbukira ine.

Mwanjira yomweyonso iye anatenga chikho, ndipo pamene iye anadya, nkuti . . . (chikho tsopano) . . . Ichi ndi chikho cha pangano latsopano mwa magari anga: izi muzichita . . . , mowirikiza pomwe muzimwa iwo, mwa kundikumbukira ine.

Pakuti mowirikiza pomwe muzidya mkate uwu, ndi kumamwa chikho ichi, inu muzisonyeza apo imfa ya Ambuye mpaka iye adze.

⁵⁷ Mukuona? Uwo ndi Mgonero. Ine ndikuzindikira ndipo ndikuvomereza kuti—thupi la Ambuye, Mawu amoyo, ndi Khristu Mwiniwake. Koma izi ndi zophiphiritsa monga ngati Ubatizo, ndi Kusambisana mapazi, ndi malangizo ena a Mpingo. Koma Mgonero uli mwamtheradi wofunikira kwa mkate, tsopano, mkate ndi vinyo.

Chomwechonso aliyense yemwe adzadya mkate uwu, ndi kumwa chikho ichi cha Ambuye, mosayenera, . . .

⁵⁸ Tsopano, funso linafunsidwa apa: “Inu potenga—inu potenga vinyo ndi zotafunira, matenda ndi tulo kukhala pa inu.” Mwaona, izo. . . ine ndikukhulupirira kuti funsola liri, kuti kupembedza kokha komwe kulipo, kuli mu Mzimu Woyera,

kupembedza mu Mzimu Woyera. Izo ziri ndendende Choonadi. Inu muyenera kumapembedza. . . Kupembedza konse mu Mzimu Woyera, ndipo Paulo akuyesera kunena apa, kuti inu muyenera kumakhala mu Mzimu Woyera musanamachite izi kapena inu mukudya ndi kumwera themberero kwa inumwini (mwaona?)—inu musanachite izi, dongosolo lisanachitidwe.

⁵⁹ Tsopano, kuti tiikire kumbuyo izo, ine ndiri nako kolembedwa apa ka Josephus, pomwe iye ankanena kuti Akhristu oyambirira pambuyo pa imfa y—ya Yesu, kuti iwo ankatengedwa ngati odyanya nyama ya anthu, chifukwa iwo ankatenga thupi la Ambuye ndi kumalidya ilo. Ndipo iwo ankaganiza kuti iwo anali atakalifukula ilo, ndipo analitulutsamo ilo, ndipo iwo anali kulidula ilo mzidutswa, ndi kumalidya ilo. Chomwe iwo anali kutenga Mgonero. Mwaona?

Tsopano, penyani, chifukwa Lemba ili—momwe Paulo akunenera apa.

Koma muloleni munthu azidzifufuza yekha, ndipo chotero muloleni iye azidya za mkate, . . .

⁶⁰ Kudya za mkate. Tsopano, ine ndikudziwa Yesu ndi Mkate wa Moyo; izo nzoona. Koma ichi ndi chophiphiritso monga ngati ubatizo. Ubatizo sumakupulumutsa iwe; ubatizo uli kokha chizindikiro kuti iwe ukuchitira umboni kwa gululo kuti iwe ukukhulupirira mu imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro cha Yesu Khristu. Iwo sumakupulumutsa iwe. Madzi sadzakupulumutsa. Ndi chikhulupiriro chako chomwe chimakupulumutsa iwe. Koma ubatizo ndi langizo, ndipo ilo liyenera kumachitidwa, chifukwa Mulungu sanganene kuti mubatizidwe, ndiyeno nkutembenuka apo nkuti sizikusowa kuti zizichitidwa. Iye sangakhoze kuikapo kutenga Mgonero, ndi kutembenuka apo, nkuti inu palibe chifukwa chomawutengera iwo. Inu muyenera kuti muzichita izo. Ilo ndi langizo kwanthawizonse ndi Mulungu.

Pakuti iye amene adya ndi kumwa mosayenera, adya ndi kumwa themberero kwa iyemwini, posalizindikira thupi la Ambuye.

⁶¹ Tsopano, inu mukuona apo? Zikubwerera mmbuyo momwe kwa Mkhristu yemwe akuyesera kuti adye Mgonero, yemwe asali mwa Mkhristu, yemwe sakuyanjana mu Mzimu; iye sali woyenera kuutenga iwo. Ndipo pamene iye atenga Mgonero uwo, iye akudya ndi kudzimwera themberero kwa iyemwini, ngati iye akumapita akusuta, kunama, kuba, kuchita chigololo, kapena chinachake chonga izo, kapena posamakhala moyo wa Chikhristu. Ndipo anthu nkumawona mtundu wa moyo womwe iye akukhala, ndiyeno nkumabwera umo, nkumatenga langizo ili la imfa n—ndi thupi la Khristu, kudzitengera mwa iye chiphiphiritso k—kut iye wamulandira Khristu Mawu mu mtima mwake, ndi kumatenga chiphiphiritso ichi apo kumbuyo

kwa izo, Iye anati iye akudya ndi kudzimwera themberero kwa iyemwini, posalizindikira thupi la Ambuye.

⁶² Tsopano, mu maminiti pang'ono ine ndikuti ndifike ku funso lomwelo, ngati ife titi tifike kwa ilo, chifukwa ndi langizo lomwelo la kuchitira mwano Mzimu Woyera. Mwaona? Chifukwa inu mukudzinenera chinachake, ndi kumachita gawo la wachinyengo ndi izo, pamene inu simukuyenera kuti muzizichita izo. Chabwino! Ndiloleni ine nditsirize izi ndiye, onani, ndiyeno ife tiima.

Pa chifukwa cha ichi ambiri ali odwala ndi ofooka pakati panu, ndipo ambiri agona.

Pakuti ngati ife tikanadziweruza tokha, ife sitikanati tiweruzidwe.

Koma pamene ife tiweruzidwa, ife timakwapulidwa ndi Ambuye, kuti ife tisadzawonongedwe limodzi ndi dziko.

Chomwecho, abale anga, pamene inu mubwera palimodzi kuti mudzadye, zidikiranani wina ndi mzake. (Tsopano, penyani.)

Ndipo ngati munthu aliyense adya—munthu aliyense amva njala, . . .

⁶³ Musati muzibwera umo. . .chifukwa mu Lemba lina apa, iwo anali akubweretsamo chakudya, ndi zakumwa zochulukwa kwambiri, ndi zinthu monga choncho, mpaka iwo ankaipangitsa nyumba ya Ambuye kungokhala—malo a—phwando, ndi kumaledzera pa gome la Ambuye. Inu mukuzikumbukira izo mu Bukhu la Akorinto umu. Iwo ankaledzera pa gome la Ambuye. Koma Paulo anati apa:

. . .ngati munthu wina amva njala, muloleni iye akadye kwawo; kuti inu musadzere palimodzi ku chiweruzo. Ndipo zinazo ndidzaziika mu dongosolo pamene ine ndidzabwera. (Mukuona?)

⁶⁴ Tsopano chotero, ine ndikukhulupirira kuti kudya kwa zotafunira. . .Tsopano, ine sindikukhulupirira kuti mkate wopatulika uzilowezetsedwa mmalo ndi zotafunira. Ine ndikukhulupirira kuti iwo uzikhala mkate wopatulika wopanda chotupitsa, choimira mkate wopanda chotupitsa womwe unkapangidwa mu Igupto. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Magazi asamakhale madzi a mpesa, koma iwo azikhala vinyo. Madzi a mpesa amanyung'unya, ndipo amawonongeka pamene iwo akhalitsa. Koma vinyo amakhala bwinoko ndi wamphamvuko pamene iye akhalitsa; iye samataya konse mphamvu yake. Ndipo Magazi a Khristu samanyung'unya ndi kuwonongeka; pamene iwo amakhaliitsa, iwo amakhala amphamvuko ndi abwinoko pamene masiku akudutsapo kwa wokhulupirira. Ndipo uyo ndi vinyo weniweni ndi mkate. Mkate

wa Mgonero uzipangidwa ndi anthu omwe adzipereka okha ndi kudzipatulira okha kwa Mulungu.

⁶⁵ Ine ndinapita ku tchalitchi nthawiina komwe iwo amadya mtanda wa mkate wakale uwu, komwe ochimwa anali akutukwana ndi kumapitiriza, ndi zonyansa, namadula mkate wakale uwo ndi kuwuika iwo apo limodzi ndi mtundu wina wa madzi azipatso kuti aziwamwa. Kwa ine izo zinali—izo zinali zopusa. Ine ndikukhulupirira kuti izo ziyenera kumakhala ndendende basi momwe Lemba linanenera kuti izo zizikhala ziri ndi mopanda kusiyana chidutswa chimodzi kwa Malemba, kukhala kumene ndi Iwo.

79. Funso. Tsopano! M'bale Branham, kodi ndi zoono kuti nthawiyina Satana anali Kumwamba ndipo anakankhidwako, iye ndi angelo ake anabwera pansu ku dziko lapansi, kapena kodi ndi masomphenya monga Yohane anawonera pa Chisumbu cha Patmo? Chifukwa chomwe ine ndikufunsira izi, ndi, ine ndinauzidwa kuti awo anali masomphenya.

⁶⁶ Yohane anawona izo ngati masomphenya, koma izo zinali zochitika zenizeni. Ngati inu mungatembenezire ku Yesaya 14:12. Tsopano, izi zikupita mochedwa, koma kwa ine, i—iwo ndi maphunziro. Ndipo ndi chinachake chomwe. . . Mwinamwake inu mukuganiza, “Chabwino, ine sindiri kuchisowa icho tsopano.” Inu simukudziwa basi momwe Mzimu Woyera umadyera pa Mawu a Mulungu. Iwo uyenera kukhala ndi Mawu—kuti uzidyerapo, chifukwa Mzimu Woyera umadya kokha, ndi pa Mawu a Mulungu okha. Inu mukukhulupirira izo? Baibulo linanena chomwecho. “Munthu sazikhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa ya Mulungu.” Chabwino! Mutu wa 14 wa Yesaya, ndipo ine ndikukhulupirira apa tsopano ife tikuti tiyambire pa ndime ya 12. Tiyeni tiwerenge tsopano za Lusifara.

Iwe wagwa bwanji kuchokera kumwamba, O Lusifara, . . . (Wagwa kuchokera Kumwamba) . . . mwana wa m'banda kucha! . . . (Chinthu chaungelo chochokera Kumwamba.)

Iwe wagwa bwanji kuchokera kumwamba, O Lusifara, mwana wa m'banda kucha! momwe iwe wadulidwira pansu, yemwe un kayenda—kuwafooketsa mafuko!

Pakuti iwe unati mumtima mwako, ndidzakwera kumwamba, ndipo ndidzakweza mpando wanga wachifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu: ndidzakhallanso pamwamba pa phiri la osonkhana, mmbali, mwa kumpoto

Ine ndidzakwera pamwamba pa mitambo yapatalitali; ine ndidzakhala monga Wammwambamwamba.

67 Chotero inu mukuwona awo sanali masomphenya. Mwamtheradi, Lusifara anathamangitsidwa kuchokera Kumwamba.

68 Tsopano, tiyeni titembenezire ku Chipangano Chatsopano ku Luka 10:18, miniti yokha, ndi kuwona zomwe Yesu ananena. Mu Bukhu la Luka, inu mutenge Mabaibulo anu tsopano, amene mukuyesera kuti mufike pa mafunso awa, Luka 10:18:

*Ndipo iye anati kwa iwo, . . . (Yesu akuyankhula.) . . .
ine ndinamuwona Satana monga mphenzi akugwa
kuchokera kumwamba.*

69 Mwaona, Satana anali mngelo wamkulu woyambirira wa Mulungu. Iye anayamba wakhalapo Kumwamba. Iye anayamba wakhalapo munthu wamkulu kwambiri kumiyamba kunja kwa Mulungu. Iye anali munthu wakudzanja lamanja la Mulungu wa chiyanjano, ndipo iye anayamba kutukumuka mu mtima mwake.

70 Ndipo kodi izo siziri mwanjira yomweyo momwe anthu akuchitira lero? Msiyeni Mulungu angomudalitsa munthu ndi kuika chidaliro pang'ono mwa iye, ndipo iye amayamba kukhala wodziwa izo zonse. Iye amafika pokhala . . . Iye amafika poyambitsa bungwe, kapena iye ayenera kuti achite chinachake chomwe chiri chosiyana. “Momwe iwe wagwetsedwera kuchokera Kumwamba, O Lusifara!”

71 Ndizo . . . Mulungu amakhala ndi nthawi yovuta poyesera kuti amupeze winawake yemwe Iye angamakhoze kumachita naye, yemwe angakhale modzichepetsa, ndi mofatsa, ndi kumakhala mu malo ake mpaka Mulungu amuitane iye kuti achite chinachake (inu mukukhulupirira zimenezo? Mwaona?), mwamuna yemwe Mulungu angamudalitse ndipo iye nkumazisungabe yekha ngati mwamuna, osati kukhala mngelo kapena mulungu. Mwamsanga pamene munthu ayamba kudalitsidwa ndipo ali ndi kenakake kakang'ono kamene kapatsidwa kwa iye, iye amafuna kuti akhale kamulungu; iye amafuna kuti akhale m—mngelo. Iye amafuna kuti akhale munthu winawake wamkulu. “Zomwe ine ndimachita, zomwe . . . Ine ndi ine ndi zanga . . .” zonse izo. Awo ndi matengedwe olakwika. Mulungu akusaka winawake yemwe Iye angadzakhoze kumudalitsa ndi kutsanulirapo madalitso, n—ndipo Iye akamamudalitsa iye mochulukuka, ndi pamene munthuyo amakhala wocheperapo.

72 Ndipo iwe sudzapeza kuchulukuka kwa Mulungu mpaka iwe utakhala kuti siwe kanthu. Iwe uyenera kuti udzichepetse wekha. Iye yemwe ati adzadzikweze yekha, Mulungu adzamutsitsa. Iye yemwe adzichepetsa yekha, Mulungu adzamukweza. Iwe uyenera kuti uchepe usanakhale wamkulu. Ndipo iwe sudzakhala konse wamkulu mwa iwewekha;

iwe udzakhala kokha wamkulu pamene Mulungu akukhala wamkulu mwa iwe. Mukuona?

⁷³ Chotero Lusifara ali pa dziko lapansi lero kuyesera kugwira ntchito mu mpingo kuti akwaniritse cholinga chomwecho chimene iye anachiyamba asanaikidwe maziko a dziko. Lusifara anakankhidwa kuchokera Kumwamba. Chabwino.

⁷⁴ Ine ndikukhulupirira pali chinthu china apa, Ezekieli mutu wa 28, ndime ya 12. Tiyeni tiwone chomwe apo zikunena mu Ezekieli 28:12. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti powerenga izi, ndi poyang'ana mu izo, kuwona chomwe chiri PAKUTI ATERO AMBUYE, ndiye ife tidziwa ngati iye anagwa kwenikweni kuchokera Kumwamba kapena ngati anali masomphenya chabe—28 ndi 12. Chabwino. Ine ndikukhulupirira ndi zomwe ine ndinazilemba apa, 28:12. Chabwino. Apa ife tikuyamba.

Tsopano, ichi ndi chinthu chachikulu apa; ine ndikukhumba ife tikadangkhalala nayo nthawi yoti tilalikirepo pang'ono pokha (mukuona?), pakuti ndi chinachake kwenikweni.

⁷⁵ Tsopano, monga ine ndangotsiriza kumene kuika maziko pa izi, kuti Lusifara Kumwamba anayesera kuti adzikweze yekha ndipo ngakhale kuti angokhala wapamwamba pang'ono kuposa Bwana wake. Ndipo iye anamupereka Mikaeli, ndipo anadzipangira yekha ufumu wawukulu kumpoto, nabwera pansu. Tsopano, ndipo iye ndi angelo ake anaponyedwa kunjia.

Munthu anafunsa za Chivumbulutso...Izo ziri pa Chivumbulutso 12, pa Chisumu cha Patmo.

Koma tsopano zindikirani izi apa, pa ndime ya 12, ndipo penyani momwe iye akukhalira mu ufumu wa munthu.

⁷⁶ Ndi anthu angati pano akumvetsa kuti mdierekezi akulamulira fuko lililonse pansu pa Kumwamba? Mdierekezi akulamulira United States. Mdierekezi ndiye boma la United States. Mdierekezi ndiye boma la Germany. Iye ndi boma la fuko lililonse pansu pa miyamba. Mdierekezi amalumulira fuko lililonse, Baibulo limati iye amatero. Werengani Mateyu mutu wa 4. Pamene Satana anamutengera Yesu pamwamba pa phiri paja, ndipo anamusonyeza Iye maufumu a mdziko, ndi kunena kuti iwo anali ake, ndipo anati, “Ine ndiwapereka iwo kwa iwe ngati iwe undipembedza ine,” Yesu sanati konse, “Iwe ukunama, Satana.” Iye ankadziwa kuti iwo anali a iye. Koma uko mu Bukhu la Chivumbulutso, anati, “Sangalalani, inu miyamba ndi inu dziko lapansi, pakuti maufumu a mdziko lino asanduka maufumu a Ambuye wathu ndi a Khristu Wake. Ndipo Iye azilumulira pa dziko lapansi.”

⁷⁷ Yesu ankadziwa kuti mu Zakachikwi kuti maboma onse ndi maufumu adzaphwasulidwa, ndipo Iye adzakhala Mulungu ndi Wolumulira wa onse awo. Iye ankadziwa kuti Iye anali woti alandire onse awo, choterono, Iye anamuza Satana, “Pita iwe

kumbuyo Kwanga, Satana!” pakuti Iye ankadziwa zomwe Iye ankati azichite.

Tsopano, mvetserani kwa izi, Mzimu wa Ambuye pa mneneri uyu Ezekieli, ukuyankhula, osati kwa mfumu iyi, koma kwa mzimu uli mwa mfumuyo. Penyani izi tsopano.

⁷⁸ Inu mukukumbukira mmawawu pamene ine ndinakusonyezani inu momwe mu Malemba kuti mpingo unapita ku njira yolakwika potenga mabungwe a anthu. Chinthu chomwecho, Israeli anachoka mu njira pakunyojetsa Mulungu monga Mfumu yawo ndipo ankafuna Sauli kuti akhale mfumu. Ndipo pamene Mfumu yawo yeniyeni inabwera, Yesu, iwo sanamudziwe Iye, chifukwa kulalikira K—Kwake ndi kuphunzitsa Kwake kunali kosiyana kwambiri ndi kwa mafumu apadziko lapansi, mpaka iwo sanali kumudziwa Iye. Ndipo lero, pamene Mfumu ya Mpingo, Mzimu Woyera, pamene Iye ali kuno, ndipo Iye akumabwera mu Mpingo kuti adzawapange anthu kuti akhale osinthika, kuti awapatse iwo kubadwa kwatsopano, izo ndi zosiyana kwambiri kwa mabungwe awa ndi zipembedzo mpaka iwo akuti, “A, izo zikuwoneka ngati oyera odzigudubuza kwa ine.” Mwaona?

⁷⁹ Izo si momwe Izo zikuwoneka kwa inu, ndi zomwe Mawu a Mulungu amanena pa izo. Yang’anani pa tsiku la Pentekoste, kodi izo zinkawoneka ngati chiani? Yang’anani pa nthawizina pamene iwo analandira Mzimu Woyera; kodi izo zinkawoneka ngati chiani? Akazi ndi amuna, namwali Maria, ndi onse a iwo, akuzandima monga anthu oledzera, akungozezedeka, kukuwa, milomo yachibwibwi, ndi malirime ena, akupitiriza ngati gulu la zidzete. Koma iwo anali akufa kwa iwoeni, ndipo Mzimu Woyera unali ukubwera mkati mwawo. Ndipo iwo analiyatsa dziko lodziwika pa moto. Chomwe ife tikusowa lero ndi anthu omwe ati afe kwa iwoeni, ndi kuvunda kwa iwoeni, ndi kuwotcha mlatho uliwonse mmbuyomo, ndi kudzipereka chirichonse kwa Khristu.

⁸⁰ Penyani Mzimu Woyera ukuyankhula tsopano kwa mdierekezi mwa mfumu iyi? Penyani yemwe munthu uyu anali amene akumutsogolera mfumu iyi.

Inu mukukumbukira zomwe ine ndinanena mmawa uwu, mkazi wanga ananena za mkazi uko, gulu lonse ilo la akazi owoneka moipa aja, atavala zovala zoipazo? Mwaona? Anati, “Iwo sayenera kuti anali mu malingaliro awo oyenera. Mkazi yemwe ali ndi malingaliro ake oyenera sangamadziyalutse yekha monga choncho.”

⁸¹ Ine ndinati, “Wokonedwa, iye wangokhala wa Chimereka; ndizo zonse. Ndi mchitidwe wa kuno. Iwo azichita izo, chifukwa uwo ndi mchitidwe.” Mwaona, iwo amachita izo mwa luntha lawo. Koma luntha lanu, ngati inu muzichita mwa mutu wanu, inu mukulamuliridwa ndi mdierekezi. Mdierekezi anatenga

mutu wa munthu, Mulungu amatenga mtima wa munthu. Mdierekezi amakupangitsa iwe kuti uziyang'ana pa chinachake chomwe iwe ungakhoze kuchiwona. Iwe nkuti, “Chabwino, uko nkulondola, uko nkulondola, lingalira, lingalira izo.” Koma Baibulo limatilola ife kuti tiponyere pansi kulingalira, ndipo mwa chikhulupiriro ife timakhulupirira zinthu zomwe ife sitimaziwona. Ndi chomwe Mulungu amachita pamene Iye abwera pa mtima wa munthu.

⁸² Mmunda wa Edeni mdierekezi anatenga mutu wa munthu; Mulungu anatenga mtima wake. Ndipo uwo ndiwo mpandowachifumu wa Mulungu, momwe Mulungu amakhala, mu mtima wa munthu. Ndipo tsopano, ngati izo ziri mwaluntha... Zedi, ndiye mwamuna kapena mkazi yemwe wabadwa mwa Mulungu azichita monga Ufumu womwe iwo akuchokerako. Aleluya! Izo zindipangitsa ine kufuula. Bwanji? Chifukwa pamene iwe udziwa kuti iwe wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo, chifukwa iwe umadana ndi tchimo, ndipo iwe umamukonda Mulungu; ndipo iwe uziima ziribe kanthu kaya ufa kapena siufa. Iwe uziima kuti izo ndi zolakwika, ndi kutchira cholakwika cholakwika, ndi kumayenda moongoka pamaso pa Mulungu. Izo zimasonyeza kuti Mzimu wako, Moyo womwe uli mkati mwako ndi wochokera ku malo ena, komwe kuli koyera, ndi kwangwiro, ndi namwali, ndi wosaipitsidwa.

⁸³ Ndipo inu mukuti, “machiritso Auzimu?” Zedi! Mzimu wanga unachokera ku malo komwe Mchiritso Wauzimu ali. Ndife ochokera ku dziko la machiritso Auzimu. Amen!

⁸⁴ Mukuti, “Inu mukukhulupirira kuti Mulungu ali.” Zedi, izo ndi ochokera ku dziko komwe Mulungu ali. Ndipo ndife amwendamnjira ndi alendo monga Abrahamu ndi Isaki. Pamene basi—kuphimba kwa Mzimu Woyera kunkawagunda iwo, iwo ankadutsa mu dzikolo ndipo ankavomereza kuti iwo anali amwendamnjira ndi alendo. Iwo anali akufunafuna Mzinda womwe wowumanga wake anali Wowupanga anali Mulungu. Ndipo tsopano, ife titakhala kale ndi Umboni wa iwo ukukhala mkati mwathu, ndi mochuluka bwanji momwe ife tiyenera kumakhala amwendamnjira ndi alendo, tikuyenda kudutsa mdzikoli, tikutembenuza mutu wathu kwa zinthu zoipa, chifukwa ndife a fuko lina, anthu ena. Ndithudi!

⁸⁵ Tsopano penyani zoipa zikulamulira dziko lino tsopano, pamene ife tikuwerenga kuchokera ku Ezekieli 28:12.

Mwana wa munthu, tenga nyimbo ya maliro kwa mfumu yaku Turo, nuti kwa iye, Pakuti Atero Ambuye MULUNGU; . . . (Tsopano penyani; Iye akuyankhula kwa mzimu uli mwa mfumuyo. Mukuona?) . . . Pakuti atero Ambuye MULUNGU; Iwe umaphimba dzuwa, wodzaza nzeru, . . . wangwiro mwa kukongola. (Satana, mukuona

apo momwe Satana anali wokongola kwambiri mwa angelo aakulu?)

Iwe unali mu Edeni. . .

⁸⁶ Tsopano inu mukudziwa Mfumu yaku Turo pa nthawi imeneyo sakanakhala kuti anali mu Edeni, pakuti izo zinali zaka zikwi zinai mmbuyo mwa apo. Mukuona? “Iwe unali mu Edeni,” kodi Iye akuyankhula kwa ndani? Iye akuyankhula kwa Satana mwa mfumu imeneyo. Aleluya! M'bale, ine ndikumverera mwachipembedzo. Liti. . .

⁸⁷ Ndiyeno, kodi anthu awa adzachita chiani omwe amachitira mwano ndi kuwatonga anthu omwe ali pansu pa chiwonetsero cha Mzimu Woyera? Pamene iwo amawatonga anthu amenewo iwo akuchitira mwano Mzimu Woyera zomwe ziri mwamtheradi zosakhululukidwa. Inu simukuyankhula za munthu ameneyo, inu mukuyankhula kwa Mzimu womwe ukuchita mwa munthu ameneyo. Iye tikuyenera kuti tizilemekezana wina ndi mzake, ndi kukondana wina ndi mzake, ndi kulimbikitsana wina ndi mzake, kuyankhula zabwino za wina ndi mzake. Ndizo zomwe ife tiyenera kumachita.

Tsopano mvetsarani kwa izi. Chabwino.

. . .Iwe umaphimba dzuwa, wodzaza nzeru, . . . wangwirowa mwa kukongola.

Iwe unali. . . mu Edeni, munda wa Mulungu; ngakhale miyala yodula inali chophimba chako, sardiyo, topazi, . . . daimondi, . . . berulo, . . . oniyzi, . . . yaspi, . . . safiro, . . . emiroidi, . . . carbankulo, ndi golidi: . . . ntchito yamanja ya chibadiri. . . ya mipope inakonzedwa mwa iwe tsiku mu lomwe iwe unalengedwa.

⁸⁸ Ndi uyo Lusifara. Iye anayamba wakhalapo mu Edeni. Tsopano, ife tibwerera kwa funso limenelo mu miniti, Lusifara mu Edeni, chifukwa ife tiri ndi mbewu ya serpente pansu apa penapake chomwe chiri chinthu cholakasa kwambiri. Ine ndimaganiza ine ndikungoyembekeza ilo liri la pafupi kotsiriza.

⁸⁹ Koma iye anali, ndipo mdierekezi anakankhidwa kuchokera Kumwamba. Ndipo cholinga chomwecho chimene iye anayesera kuchilinga Kumwamba, iye anabwera pansu pomwe kuno ku dziko lapansu ndipo iye akuyesera mwakukhoza kwake kuti akwaniritse zomwe iye ankalinga izo. Iye amapita kwa mafumu ndi kwa olamulira, ndipo pamene iye angakhoze kuwatenga iwo, ndiye iye amabwera pansu pomwe kwa mpingo ndi kuwatenga anthu—kapena kumutenga mlaliki. Ndiye kuchokera kwa mlaliki, iye amapita mpaka mwa osonkhana ndipo amawatengera osonkhanawo pansu pa kukopa komweko, mdierekezi yemweyo akuchita zinthu zomwezo. “Inu mukudziwa, inu ndinu a Chipresbateria, inu simudzakhala konse woyera wodzigudubuza. Ndinu *ichi, icho*, kapena *chinacho*; inu simungakhoze kukwanitsa kudziyozetsa nokha

kuti muzikhala pakati pa iwo. Bwanji, inu mumadziwa bwino kuposa kumakhala mu mmodzi wa makachisi awo kapena mishoni ya pa msewu. Bwanji, anthu awo ndi osokonezeka mutu.” Ayi, iwo sali. Ayi, iwo sali; iwo angokhala bwino mu mtima wawo; ndizo zonse. Iwo sanasokonezeke mutu wao; iwo akungolamuliridwira mu mtima wawo. Mulungu akukhala mu mtima mwawo, ndipo iwo ndi anthu achilendo, aunsembe wachifumu, opereka nsembe zauzimu; ndizo zipatso za milomo yawo popereka matamando kwa Mulungu, kaya iwo akumverera ngati choncho kapena ayi. “Nthawi zina ine sindimamuwona Iye,” anatero wolemba nyimbo, “Ine ndimadalira ndi kumamupatsa Iye matamando.”

⁹⁰ Mukuti, “Chabwino, ine ndikanapita ku mpingo, ndipo ine ndikanawayamika Ambuye ngati ine ndikanamverera kuti nditero.” Chabwino tsopano, wansembe ndi woti azipereka nsembe. Ndipo inu, osonkhana, ndinu ansembe aakulu a Mulungu, oti muzipereka nsembe zauzimu; ndizo zipatso za milomo yanu popereka matamando kwa Mulungu.

⁹¹ Inu mumapita uko kumati, “Chabwino, ngati ine ndikanamverera munga chomwecho, ine ndikanapita ndi kukachitira umboni kwa winawake.” Chabwino, zichitani izo mulimonse! Ngati inu muli wansembe wamkulu, m’bale, Izo zizikuwotchani mu mtima wanu, kaya inu mukumverera ngati muchite izo kapena ayi. Pitani muzikachita izo mulimonse, chifukwa inu muyenera kuti mupange nsembe, chinachake chomwe chiri chovuta kuchichita. Pitani muzikachita izo mulimonse, ndinu unsembe wauzimu, anthu achifumu, mukupereka matamando kwa Mulungu, chifukwa Mulungu akukhala mu mtima mwanu.

⁹² Tsopano, ngati inu muli wa Satana, inu mumamverera kuti inu muli bwinoko basi kuposa gulu la anthu ilo. Tsopano, inu muzidziwa bwanji chomwe chiri cholondola? Muzizitenga izo mwa Malemba. Ngati munthu wabadwa mwa Mulungu, iye amawakhulupirira Mawu aliwonse omwe Mulungu anawalemba, ndipo amati Iye ali wamkulu basi lero munga Iye nthawizonse anali, ndipo iye samasintha konse, ndipo Iye ali chimodzimodzi basi dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ngati iye wadzazidwa ndi Mzimu Woyera, iye ali nawo Mzimu Woyera womwewo umene Iye anaupereka pa tsiku la Pentekoste, ndipo umamupangitsa iye kumachita mwanjira yomweyo ndi kumachita zinthu zomwezo. Ngati iye wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu, Marko 16, Yesu anati, “Zizindikiro izi zizidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Nzoona! Chotero iye akuti, “Ndine wokhulupirira,” ndipo zizindikiro izo zikamapanda kuwatsatira, ndiye iye ndi wodzipangitsa kukhulupirira, osati wokhulupirira.

⁹³ Iipo mitundu itatu ya anthu, wokhulupirira, wodzipangitsa-kukhulupirira, ndi wosakhulupirira. Ndipo awo ndi magulu

atatu okha omwe alipo. Odzipangitsa-kukhulupirira ambiri; alipo okhulupirira enieni ochuluka; ndipo alipo osakhulupirira ochuluka. Koma ngati iwe uli wokhulupirira weniweni, Yesu anati, “Zizindikiro izi zizidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Mu Dzina Langa iwo azidzatulutsa ziwanda, kuyankhula ndi malirime atsopano. Ngati iwo ati adzaponde pa njoka (M’bale Evans) iyo siidzawapweteka iwo. Ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo azidzachira!” O, izo nzoona basi monga Mawu a Mulungu ali owona. Ife tiribe ntchito yochotsera chirichonse kwa Iwo. Baibulo linati iye amene ati adzachotsere kapena kuwonjezera kwa Mawu awa, zomwezo zidzachotsedwa mu Bukhu la Moyo, kwa iye. Mulungu ndi wangwiro kwambiri, moti mawu aliwonse ayenera kuti azikhala angwiro ndipo ayenera kuti aziyenderera kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso mofanana, mawu aliwonse, lamulo lirilonse la Mulungu. Tsopano, inu mukhoza kuzipangitsa Izo kuti zizinena chinachake apa ndi kuchipotoza Icho cha apa.

⁹⁴ Ine ndinali nditakhala tsiku lina pansi pa mtengo ndi M’bale Charlie kumtunda uko ndi M’bale Wood kuno; ife tinali tikusaka uko mu Kentucky. Ife tinali tikusaka ndi mfuti. Ndipo i... M’bale Charlie ndi M’bale Wood anali atawombera zomwe anaziwona mmawa umenewo. Pafupi mayadi 50 iwo anali akumenya malo aakulu pafupi chomwecho kuzungulira kwake, aakulu ngati gologoloyo. Iwo ankati, “Izo ziri bwino.”

⁹⁵ Ndipo ine ndinapita uko... Ine ndinali ndikuwombera timbendela pa mayadi 50. Ndipo ine ndinaphonya diso la gologoloyo ndipo ndinamumenya iye pa tsaya. Ine ndinati, “Uko si kulondola; mfuti yanga yasokonezeka.” Ndiyeno ine ndinadandaula utali wa tsiku lonse. Usiku wotsatira ine ndinalowala moyambirira. Ine ndinawombera mabokosi a zipolopolo. Ine n... Icho chinkakhoza kugundapo pang’ono pokha, theka la inchesi chakumanja. Bwanji, icho chimakhala chitamumenya gologolo pa mutu mulimonsebe.

⁹⁶ Chotero Charlie ndi iwo, mmawa wotsatira anali uko, ndipo mifuti inkangolindima, ikumangowamenya agologolo, ndipo ine nditakhala kuseri kwa mtengo ndikungosisita manja anga, ndikuti, “O, chavuta nchiani ndi mfuti yanga?” Ine ndinadzichitira manyazi ndekha, mpaka ine ndinagwada pa maondo anga, ine ndinati, “Ambuye Mulungu, ine sindikudziwa chomwe chiri vuto ndi ine. Bwanji Inu munandipanga ine, munthu wodandaula wamanjenje, wamng’ono? Nchifukwa chiani ine ndiri chonchi? Apo pali anthu awo akuwombera agologolo, zolimba basi monga iwo angakhoze kuwombera. Iwo ali ndi mulu wa agologolo okwanira kale, ndipo pano ine ndiri, nditakhala kuseri kwa mtengo, ndikusisita manja anga, ndi kumadabwa, ‘Mai—mfuti yanga sikuwombera molondola, pa mayadi makumi asanu.’” Ine ndinalira, nditakhala apo pambali ya chipika.

Ndiyeno Mzimu Woyera unadza, osati mwa Liwu, koma mwa vumbulutso, unati, “Ine ndinakupanga iwe mwanjira imeneyo kwa cholinga.”

⁹⁷ Bwanji? Ine sindingakhoze kutenga Baibulo likunena chinachake apa, monga mpingo umanenera, “Mzimu Woyera unali wa kagulu kaja kokha mmbuyo umo,” mpingo umanena chomwecho; ndipo Lemba limati, “Aliyense yemwe afuna.” Ine sindingakhoze kupanga izo kugunda chandamale.

⁹⁸ Ine sindingakhoze kupanga Chikalvini—kungokhulupirira pa Ambuye ndipo inu muli nacho chitetezero chamuyaya—ndi Chiarmeniani, “Kuti ngati ine nditangoti ndisakhudze, ndisagwire, ndisalawe, i—ine ndimafuna nditachita izo, koma ine sindingakhoze kuchita izo!” . . . Chiarmeniani chiri kutali kwambiri ndi Chikalvini, ndipo iwo onsewo ndi olakwitsa. Ine ndiyenera kuti ndiwone pamene . . . Iwo onse ali nawo Malemba, koma izo ziyenera kumagunda pa chandamale. Tsopano, ngati Mulungu ananena chinthu chimodzi mu Baibulo ili, icho chiyenera kumagunda chandamale; icho chiyenera kumapanga kulira kulikonse mu Baibulo ilo kubwera molunjika kumene ku diso la ng’ombe ilo. Izo ziyenera kuti zichite icho, chifukwa Awo ndi Mawu a Mulungu; ndipo Iye ndi wopandamalire, ndipo Iye sangakhoze kusintha. Amen! Ine ndikuzikonda izo, chifukwa ndiye iwe ukhoza kupuma utakhutitsidwa mwangwiro kuti Awo ndi Mawu amuyaya a Mulungu. Ndipo chotero, ine ndimayesa kuwerenga Izo kuchokera ku Malemba osiyana kuti ndizipange Izo—ndiwone chomwe Izo zikanati zinene. Chabwino.

⁹⁹ Satana anakankhidwa kwenikweni kuchokera Kumwamba ndi Mikaeli Mngelo wamkulu ndi Mulungu. Ndipo iye anaponyedwera ku dziko lapansi, anabwera ku dziko lapansi, anadalowa mwa serpenti, anamunyenga Eva, ndiyeno walowa mwa amuna, akazi, mmusi monse kudutsa mu m’badwo pa chinthu chomwecho chimene iye anachiyamba pachiyambi—ufumu wawukulu kwambiri, wokongolerao kuposa wa munthu winayo, kukhala kazembe wa pamwamba pa zonse, wodziwa zonse. “Chipembedzo chathu ndi chachikulu kwambiri; ndi—ndi—cholamulira pamwamba pa zinazi.”

¹⁰⁰ Inu mwawamvapo iwo akuti, “Bwanji, ife tiri nawo alaliki mazana ochuluka chotero mu bungwe lathu. Ife tiri nayo mipingo yaikulu kwambiri yomwe ilipo mu mzinda.” Chinthu chimodzi chokha chomwe izo zimatchula ndi S-a-t-o-n kwa ine. Ndiko kulondola. Izo zimatanthauza mdierekezi kwa ine. Pamene inu mumpeza munthu yemwe angaswe zinthu ndi kupanga bungwe, ndi kuswa ubale, nkuti iwo sadzakhala ndi chochita nao chirichonse mpingo wawung’ono . . .

¹⁰¹ Ine sindinayambe ndamuwonapo munthu wotsika kwambiri panobe, kapena ine sindinayambe ndamuwonapo munthu wotaika kwambiri mu tchimo panobe; ine sindinayambe

ndamuwonapo mmodzi—mkazi wotsika kwambiri kapena mwamuna wotsika kwambiri, koma yemwe ine ndikanati ndipite kwa iye, ndi kukaika mikono yanga momukumbatira iye, ndi kumuchotsa iye mu izo ngati ine ndingathe. Ine sindinayambe ndawonapo gulu la oyera odzigudubuzwa, kapena chirichonse chomwe inu mukufuna kumawatcha iwo, kuzika, ndi kumalumpha, ndi kumakuwa, kapena chirichonse chomwe iwo akanati azichita, koma omwe ine ndingafike umo momwe ndi kumazika, ndi kulumpha, ndi kukuwa limodzi nawo kuti ndimulemekeze Mulungu (ndizo ndendende kulondola!) kaya iye ndi wakuda, wachikasu, wabulauni, woyera, kapena chirichonse chimene iye angakhoze kukhala ali. Inde, bwana!

¹⁰² Mzimu Woyera umabwera pa muyezo umodzi; nkuti iwe wakwaniritsa chofuna cha Mulungu. Ngati iwe utawulandira konse Iwo, iwe umafika pa muyezo wa Mulungu ndipo osati malingaliro ako ako a Iwo. Satana amayesera kuti azipangitse izo kukhala za mwapamwamba, chinachake chopambana, chinachake chachikulu, luntha. Iwe umayenera kuti uponyere pansu kulingalira uko ndi kukhulupirira chomwe Mawu amanena pa izo. Amen!

80. Tsopano, pano pali limodzi lina; tiyeni tiwone chomwe ilo liri. Chabwino. **Chonde tafotokozani fanizo la anamwali asanu. Kodi Mkristu amachimwa?**

¹⁰³ Tsopano, fanizo la anamwali asanu—kapena anamwali khumi liri, chonde ndikhululukireni ine. Anamwali khumi amapezeka mu Mateyu 25:1. Anamwali khumi anapita kunja kuti akakomane ndi mkwati (tsopano zindikirani!), ndipo asanu a iwo anali anzeru ndipo anali ndi mafuta mu nyali zawo, asanu anali opusa ndipo analibe mafuta mu nyali zawo. Pamene iwo anali kugona, mfuu—mfuu unadza, “Pitani mukakomane naye mkwati.” Ndipo iwo omwe anali ndi mafuta mu nyali zawo, anakonza nyali zawo, moto unali ukuyaka, ndipo iwo anatulukira kuti akakomane naye mkwatibwi. Enawo anabwera kuti adzagule mafuta, ndipo iwo anawauza iwo kuti apite ndi kukapeza m—mafuta kuchokera kwa iwo omwe ankawagulitsa iwo. Pamene iwo anali kupita, mkwatibwi anadza n—namwali wochenjera analowa mkati, ndipo namwali wopusa anaponyedwa kunja.

¹⁰⁴ Izi zipweteka, kupweteka kwenikweni, koma ine ndiyenera kuti ndizinene izo basi. Ine sindinalifunse konse funsolo; ine ndingokhala ndi udindo wakuliyankha ilo. Tsopano, izi zikubwera pafupi kwambiri ndi kwathu, m’bale, pafupi kwambiri, mpaka ine ndikuyembekeza kuti izo zithandiza mmalo mopweteka. Kawirikawiri iwe umayenera kuti upweteke...Monga amayi anakonda kunena pamene iwo akundikwapula ine, iwo ankati, “Icho chimayenera kuti chipweteke icho chisanakuchitire iwe ubwino.” Chabwino, u—

uko nkulondola. Mwaona? Ine sindinkakhoza kuziwona izo apo, koma i—ine ndikuziwona izo tsopano.

¹⁰⁵ Penyani, o... Onse khumi a iwo omwe anapita kunja anali anamwali. Tsopano, panali anamwali khumi anapita kukakomana ndi Ambuye. Tsopano, mawu oti *namwali* amatanthauza “woyeretsedwa (kodi aliyense amadziwa zimenezo?), woyera, wangwiro, woyeretsedwa.” Panali khumi a iwo omwe anapita kunja kuti akakomane ndi Ambuye.

¹⁰⁶ Tsopano kumbukirani, iwo anali akugona mu ulonda umodzi, ulonda wachiwiri, ulonda wachitatu, kupitirira mpaka ulonda wachisanu ndi chiwiri. Koma awa anapitadi kuti akakomane ndi Ambuye. Ndipo kumbukirani, pamene iwo anali kupita, Ambuye anadza. Iyo inali nthawi ya kubwera kwa Ambuye. Osati omwe anali mu ulonda...

¹⁰⁷ Yesu anayankhula pomwe ena anagwa mu ulonda woyamba, ndi ena mu ulonda wachiwiri, ndipo ena mu... Koma pa kudza kwa Ambuye iwo onse anawukitsidwa. Koma pa nkhani iyi, uwo unali ulonda wotsiriza, chifukwa iwo anatuluka, khumi a iwo, kuti akakomane ndi Ambuye. Ndipo asanu anapangitsa utsi nyali zawo, ndipo sanatenge mafuta; asanu anali nawo mafuta.

¹⁰⁸ Tsopano kumbukirani, mafuta mu Baibulo ndi chophiphiritsa cha chiani? Kodi wina aliyense anganene? [Osonkhana ayankha, “Mzimu Woyera”—Mkonzi.] Mzimu Woyera! Ndiye iwe ukhoza kukhala woyera, ndi wangwiro, ndi woyeretsedwa popanda kukhala nao Mzimu Woyera. Kuyereetsa ndi chimene iwe uli...

¹⁰⁹ Tsopano penyani, ine ndikuti nditenge monga ngati botolo ili. Ndipo ilo liri kunja uko ku khola la nkukuku, ndipo lonse langodzaza ndi nyansi. Ine ndikalitola ilo; uko ndi kulungamitsa: “Ine ndikuti ndimugwiritse ntchito wochimwa uyu.” Ndipo chinthu chotsatira chomwe ine nditachite ngati nditi ndiligwiritse ntchito ilo, ine ndisowa kuti ndilitsuke ilo. Ndiyeno, ngati ine ndilitsuka ilo, kodi ine ndichita chiani kwa ilo? Kuliyeretsa ilo. Mawu okuti *sanctify* kupanga—amatanthauza “kuyera,” chinthu chofanana monga kuyera. *Woyera—woyera* ndi mawu Achigriki, *kuyereetsa* ndi mawu Achigriki. Mawu oti *kuyereetsa* amatanthauza “kutsuka ndi kuchiika pambali kuti chitumikire.” Komano, odala ali iwo amva njala ndi ludzu la chilungamo pakuti iwo adzakhutitsidwa, ndiye iwo amaikidwa mu utumiki.

¹¹⁰ Zida... Kachisi wa Chipangano Chakale, guwalo linkayeretsa zotengerazo, ndipo izo zinkaikidwa pambali kwa utumiki. Pamene izo zinali kudzazidwa, izo zinali mu utumiki.

¹¹¹ Tsopano, apo ndi pamene inu okonedwa, Anazerini ofunika ndi ena otero, munasiya chikhomo. Mwaona? Ife tonse... Nchifukwa chiani inu mukulephera? Nchifukwa chiani Chipentekoste chinathawira kwina ndi kukusiyani

inu? Chifukwa inu munakana kuti muziyenda mu Kuwala. Ndizo ndendende kulondola. Mwaona? Ndizo ndendende. Guwa loyamba lomwe ine ndinayamba ndagwadapo linali ku guwa lofunika, lachikale la Chinazarene kumusi kuno. Mulungu awadalitse iwo, mpingo wabwino, woyera, wawukhondo, koma ndinu amwamalamulo kwambiri mwakuti inu mumayendera, “Iwe uyenera kuti uzichita *izi*, ndi iwe uyenera kuti uzichita *izo*. Iwe uyenera kuti uzichita *izi*,” ndipo simumazindikira kuti ndi chisomo cha Mulungu ndipo iwe unaitanidwa mwa kusankhidwa. Si iye amene afuna kapena iye amene athamanga, koma ndi Mulungu yemwe amasonyeza chifundo. Mwaona? Mulungu anaukonzeketseratu Mpingo asanaikidwe maziko a dziko (ife tiri nalo funso pa izo mu maminiti pang’ono. Mwaona?), anaukonzeketseratu Mpingo asanaikidwe maziko a dziko.

¹¹² Inu simungakhoze, pakuganiza, kuwonjezera utali kwa usinkhu wanu. “Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba.” Mukuona? Mwaona, izo anali Mulungu yemwe anachita kuitanako, Mulungu yemwe anachita kukokako, Mulungu yemwe anaukhazikitsa Mpingo. Tsopano, tsopano, inu mukuti, “M’bale Branham, icho ndi Chikalvini changwiwo.” Ayi, sindicho. Tsopano, dikirani! Ine sindikukhulupirira kuti Mulungu amamutenga munthu apa ndi kungoti, “Apa, ine ndikutenga iwe ndi. . .”

¹¹³ Achibaptisti onse awa ndi Achipresbateria nkumati, “Chabwino, ine ndimakhulupirira pa Ambuye, ine ndiribe—sizimachitsutsa chikumbumtima changa!” Palibe zodabwitsa, inu mulibe chinthu chirichonse choti chikutsutseni. Iwo amati, “Chabwino, kuvina sikumandipweteka ine. Kumwa pang’ono chakumwa chosangulutsa sikungandipweteke ine.” Chifukwa mulibe kanthu mkati umo koti kapwetekedwe. “Kunena nthabwala zonyansa sikungandisautse ine.” Chifukwa chiani? Mulibemo kalikonse umo koti kapwetekedwe.

¹¹⁴ Koma ine sindimawatumikira Ambuye chifukwa ine ndikuganiza iye akanati anditumize ine ku gehena ngati ine ndikanati ndisatero; ine ndimamutumikira Iye chifukwa ine ndimamukonda Iye. Ine ndimamutumikira Iye chifukwa muli chinachake mkati mwanga. Ngati inu mungapite kunjako ndi kumati, “Chabwino, ine ndiyenera kuti ndisiye kuchita izi chifukwa mpingo wanga sumakhulupirira mu izo,” inu mukungosewera gawo la wachinyengo. Ndiko kulondola. Koma ngati inu mukuchita izo chifukwa chakuti i—inu mukuzikonda izo, n—ndipo ndi chothandizirapo kwa Mulungu, ndi chinachake mu mtima mwanu chikupangitsa chikondi cha Mulungu kukhala chachikulu kwambiri kwa inu kuposa zinthu izi, tsopano inu muli pa mzere wolondola. Koma ngati ine sindiri kumwa, kusuta, kutafuna, kutukwana, kusachita china chirichonse, ine ndikhoza

kupitabe ku gehena. Zedi! Ine ndinajowina mipingo yonse, ndinabatizidwa, ndiri nalo dzina langa pa mabuku onse, ndipo ndinachitapo gawo labwino, ndipo ndinakhala moyo wabwino, “Kupatula munthu akhale atabadwa kachiwiri, iye sangakhoze ngakhale kuwuwona Ufumu wa Mulungu.” Uko nkulondola!

115 Tsopano anamwali awa, khumi a iwo anachedwa nazo. Chimene chinawapunthwitsa anthu Achinazerini chinali ichi: Chifukwa Achipentekoste anatenga umboni woyambirira wa Mzimu Woyera kuti ndi kuyankhula mmalirime. Ankawatengera iwo pa guwa ndi kuwapangitsa iwo kumanena chinachake kapena chinzake mobwereza bwereza mpaka iwo atayankhula mu malirime. Wachipentekoste weniweni, woona sangakhoze kutsatira izo. Mdierekezi anali nazo zinthu zambiri mu mpingo wanu wa Chinazereni nanunso. Mwaona? Ndipo iye ali nazo zinthu zonsezo mu mpingo wa Chipentekoste, koma kukamba za ubatizo wa Mzimu Woyera, icho ndi Choonadi. Icho ndi ndendende Choonadi.

116 Pali ochuluka a iwo, ine ndikudziwa. Ine ndawamvapo anthu akuyankhula mu malirime. Ine sindingakhoze kuweruza; ine sindinatimidwe kuti ndiziweruza. Ine ndamva zambiri za izo; zimamveka ngati mkuwa wa phokoso ndi ziwaya zogundana. Koma ine ndikudziwa pali Mzimu Woyera weniweni umeneyo umayankhula ndi malirime. Ndipo ine ndikudziwa uko ndi kulondola. Inde, bwana!

117 Koma iwo anawawona anthu akubwera umo ndi kumati, “Ulemerero kwa Mulungu, ine ndaulandira Iwo.” Chabwino ndiye, icho nchinthu chomwecho... Tsopano, musamawatche awo Achipentekoste chifukwa iwo analumphwa mmwamba-ndipansi, ndipo anayankhula mmalirime, ndipo inu munawawona iwo kunjira uko ali ndi mkazi wa winawake kapena mwamuna wa winawake.

118 Inu mukuti, “Kodi umenewo ndi Mzimu Woyera?” Inu Achinazerini munkafuula pansi ponsepo ndipo munachita chinthu chomwecho. Inu munkati inu munali nawo Iwo pamene inu munafuula. Mukuona? Palibe njira nkomwe yomwe inu mungakhoze kutsimikizira izo—koma ndi moyo wanu womwe inu mumakhala. “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Ndi momwe izo ziliri. Moyo waumulungu ndi Khristu akugwira ntchito nanu kutsimikizira Mawuwo, zizindikiro ndi zodabwitsa zikutsatira ndi moyo waumulungu, ndicho chinthu chenicheni. Tsopano, inu mukhoza kukhala nazo zizindikiro zochuluka ndi kusakhala moyo. Inu mukhoza kusanzira moyo popanda kukhala nazo zizindikiro, koma pamene inu muziwona zonse izo palimodzi, ndiye ndi chimenecho. Ndi ameneyo.

Tsopano! Ndiyeno, kumbukirani, Mkwatibwi... Tsopano ine ndikhoza kutsirizitsa izi ngati inu mwangotsala ndi nthawi ya maminiti pang'ono, kupita pa izo.

119 Penyani, mkazi akamadula za diresi. Iye amakhala ndi chidutswa chachikulu cha nsalu. (Tiyeni tiyitche iyo chiani? Biliwita, guta, kapena chinachake chimzake, mtundu wina wa dzina lomwe inu muli nalo. Tiyeni tinene kuti ndi silika.) Ndipo iye ali ndi patani. Ndipo iye amayang'ana pa chidutswa chachikulu ichi cha nsalu. Tsopano, izo ziri kwa iye pomwe ati ayike patani iyi. Ndi kulondola uko? Iye akhoza kusankha iyo kuchokera pa gawo lirilonse la nsalu iyi, ndipo nsalu yonseyo ndi yochapidwa, iyo ndi yoyera. Mwaona, uko ndi kusankha. Kusankha kwa Mulungu. Chotero kodi Iye amachita chiani? Mulungu amatenga mwa kusankha ndipo amaika patani iyi ya Khristu paliponse pomwe Iye akufuna kutero pa nsaluyo. Ndiye iyo imadulidwa. Nsalu ina yonseyo ndi yoyera basi momwe gawo ili linali loyera, koma mwa kusankha Mulungu anapanga kusankha Kwake asanaikidwe maziko a dziko. Kodi Paulo sanati mu Akorinto 8—ine ndikutanthauza, Aroma 8, kuti—“Kodi wowumba—kodi dongo linganene kwa Wowumba, bwanji inu mwandipanga ine chotere?” Kodi Mulungu, Yemwe ali wolungama, pamene Iye akanakhoza kunena kwa Esau kapena Yakobo mwana aliyenseyo asanabadwe asanachite chabwino kapena choipa, “Ine ndamuda Esau ndi kumukonda Yakobo”? Ndi chifukwa mwa kudziwidwiratu Iye ankadziwa chomwe Esau anali ndi chimene Yakobo anali. Iye amadziwa chomwe chiru mwa munthu. Asanaikidwe maziko a dziko Iye anadziwa, Iye. . .

120 Ngati inu mungakhoze kufotokoza mawu oti *kupandamalire*. . . Mwa mawu oti *kupandamalire*. . . Ine ndikuti pakhala pali matani handiredi bilioni a atongole mu dziko (omwe sangayambitse izo), matani handiredi bilioni a atongole mu dziko, ndipo aliyense wa iwo aphethira diso lake nthawi ka handiredi bilioni trilioni. Ndipo palibe mmodzi wa iwo anayamba waphethirapo diso lake koma yemwe Mulungu anamudziwa asanaikidwe maziko a dziko. Ndiko kupandamalire. Icho ndi chinachake pa dongosolo la kupandamalire. Mwaona?

121 Iye ndi wopandamalire. Chotero asanaikidwe maziko a dziko Iye ankadziwa ndendende basi zomwe inu mukanati mudzachite. Ndipo Iye anatumiza Khristu, osati kuti adzangokhala. . . Ngati winawake, “Chabwino ngati ine nditangosiya nkha zanga ndi kumamutsatira Iye,” kapena chinachake chonga izo, si zimenezo. Iye ankadziwa yemwe akanati adzapulumutsidwe, chotero Iye anamutumiza Khristu kuti adzapulumutse izo zomwe Iye anaziwoneratu kuti zikanadzapulumutsidwa. Ndi kulondola ndendende.

122 Tsopano, Mpingo Iwo weni uli nacho chitetezero chamuyaya. Ngati inu muli mu Mpingo, inu mumatetezeka ndi Mpingo. Koma pamene inu mupita kunja kwa Mpingo, inu simuli otetezeka. Mwaona? Tsopano, inu muzikhala mu Mpingo.

123 Inu mumalowa chotani mu Mpingo? Kulumikizana manja, kulemba dzina lanu pa bukhu? Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi; ndiwo Mpingo. Chotani? Kupyolera mu ubatizo wa Mzimu Woyera ife timasindikizidwira mu Thupi la Khristu. Mpaka liti? Mpaka tsiku la chiwombolo chanu. Aefeso 4:30, “Musati muwukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.” Kusindikizidwira kwina mpaka tsiku la chiwombolo chanu. Tsopano. Ndithudi, ndithudi, ndiwo Mzimu Woyera.

124 Ndipo tsopano, Mpingo uwo unatengedwera mmwamba, ndi otsalira a mbewu ya mkazi omwe amasunga malamulo a Mulungu ndipo ali ndi chikhulupiriro mwa Yesu Khristu (mwaona?), osati Mkwatibwi, otsalira a mbewu ya mkazi. Ndiye chinjoka chinalavula madzi kuchokera mkamwa mwake kuti chipange nkondo ndi otsalira a mbewu. Apo ndi pamene mpingo wa chiprotestanti pansi pa Chitaganya cha Mipingo, chomwe chiri chifano kwa chirombo, chomwe tsopano chiri kupangidwa... Ndipo padzakhala kuwukira pa mipingo yonse yonga iyi.

125 Momwe ife tiriri osonkha msonkho aakulu pakali pano tsopano, mtsutsano, akuyesera kunena kuti sindife mpingo, ndipo ife tiri nao ufulu wa chikalata chotivomerezetsa kuti tizinena kuti ife ndife mpingo. Bola ngati Chivomerezetscho chikuyima apo, palibe kukonza kwa icho, ndiye mwamtheradi ife tiri nawo maufulu, ufulu wochuluka basi monga aliyense. Makolo athu ankaimira zimenezo. Koma kodi ife tachita chiani, ife taswa lamulo la Chivomerezetscho lirilonse lomwe iwo angakhoze kuliswa, ndipo posakhalitsa Chitaganya cha Mipingo, chomwe mipingo yonse ndi zipembedzo alikuitanidwirako, ndipo mdierekezi walowa umo ndipo akupanga za chidziko ndi chirichonse mwa membala a mpingo uliwonse ndi zina zotero monga choncho, ndi magulu aakulu, ndi upamwamba, ndi ziyanjano, pamene mpingo wawung’ono wakale uwo ukadali kutali uko ukubadwa kachiwiri mu nyansi monga kubadwa kulikonse, akulipirabe mtengowo, akupitabe pansi ndi kumafapo, kumachita mwanjira yomweyo momwe iwo ankachitira pamene iwo ankabadwa poyamba pa tsiku la Pentekoste, mtundu womwewo wa mpingo kumeneko... Iwo adzatsekedwa ndi kutsekeredwera kunjani pansi pa Chitaganya cha Mipingo. Kudzakhala kuli chiukiro monga mgwirizano kapena chinachake. Inu mwina mudzalowa umo kapena inu mudzapita kunjani.

126 Chilemba cha chirombo chikuchitika lero, ndipo—Chisindikizo cha Mulungu ndi Mzimu Woyera. Kuchikana icho ndi chilemba cha chirombo. Aliyense yemwe awuwona Mzimu Woyera, womwe inu mukuyenera kuti muulandire Iwo, ndipo nkusazichita izo, pomwepo inu mumatenga chilemba cha

chiroombo, chifukwa pali magulu awiri okha oti akhalepo: onse omwe analibe Chisindikizo cha Mulungu anali ndi chilemba cha chiroombo. Kotero kulandira Chisindikizo cha Mulungu ndi kulandira Mzimu Woyera. Kuwukana Iwo ndi kukhala nacho chilemba cha chiroombo. Icho ndicho chinthu chonsecho. Uko nkulondola ndendende.

¹²⁷ Tsopano, Mkwatibwi anapita mmwamba, otsalira anatsala kuno. Ndipo uyu ndi yemwe anabwera mu chiukitsiro chachiwiri. “Wodala ndi woyera ali iye yemwe ali nao gawo mu chiukitsiro choyamba, kwa omwe imfa yachiwiri ilibe mphamvu.” Uko nkulondola. Chiukitsiro chachiwiri chidzakhala Chiweruzo cha ku Mpandowachifumu Woyera, ndiye mpingo... “Kodi inu simukudziwa,” anatero Paulo, “mukupita pakati pa osakhulupirira ndi azamalamulo ndi ena otero pamene oyera ati adzaliweruze dziko lapansi.” Nkhani izi ziziweruzidwa pamaso pa Mpingo, osati pamaso pa oweruza milandu osalungama ndi ena otero, koma pamaso pa Mpingo nkhani zathu zizikhala. Apo inu mukutengerana wina ndi mzake ku lamulo. Ndipo Mulungu amchitire chifundo munthu yemwe angati amutengere Mkhristu ku lamulo. Ndiko kulondola. Paulo anati asayerekeze iwo ngakhale kuchita izo.

¹²⁸ Tsopano, uyo ndi Mkwatibwi, ndipo uko akupita namwali wogona, atasiyidwa pa dziko lapansi. Namwali wanzeru akupita Kumwamba ali ndi mafuta mu nyali yake.

Ine ndikudziwa inu mukanakhoza kutenga nthawi yochuluka pa izo, koma ine ndiyenera—Ine ndikuti ndifulumire kuti nditsirizitse izi.

¹²⁹ “Kodi Akhristu amachimwa?” Mwamtheradi ayi! Palibe Lemba pomwe Mkhristu amachimwa. Iye sangakhoze kuchimwa. Ine ndikudziwa pali kusazikonda izo. Chabwino, ife tingopita ku 1 Yohane 3 ndi kuwona chomwe Lemba likunena. Mkhristu samachimwa.

¹³⁰ Kodi inu munayamba mwaiwonapo mbalame yakuda, yoyera kapena mbalame yoyera, yakuda? Kodi inu munayamba mwamuwonapo munthu woledzera, mosaledzera? Ayi! Inu simunayambe mwamuwonapo wochimwa, woyera. Palibe chinthu choterocho.

¹³¹ Tsopano, ngati izi zifika pokhala mokhudza pang’ono, inu mungoikamo mvunguti wochuluka mmenemo, inu mukudziwa, ndipo i—izo zichira mu kanthawi pang’ono pokha tsopano.

¹³² Tsopano, Malemba ali mwamtheradi, zitsimikiziro zathu zosalephera za zomwe ife tikuzikambazi. 1 Yohane mutu wa 3 ndi ndime ya 9. Chabwino, mvetserani kwa izi!

Iye amene amachita tchimo ndi wa mdierekezi; pakuti mdierekezi anachimwa kuchokera kuchiyambi. Kwa cholinga ichi Mwana wa Mulungu anawonetseredwa, kuti iye akhoze kuwononga ntchito za mdierekezi.

Mvetserani, kodi inu mwakonzeka? Valani majekete anu, zida mutazimangira yense? Mvetserani mwatcheru, chifukwa izi ndi zogwedeza.

Aliyense yemwe ali wobadwa ndi Mulungu samachita tchimo;... (Nanga bwanji izo?)... pakuti mbewu yake... (mbewu Yake, ya Mulungu.)... imakhalabe ili mwa iye:... (Munthuyo!)... ndipo iye sangakhoze kuchimwa, chifukwa iye ndi wobadwa ndi Mulungu.

Mwa izi ana a Mulungu amawonetseredwa, ndi ana a mdierekezi: aliyense yemwe samachita chilungamo si wa Mulungu, ngakhalenso... yemwe samamukonda m'bale wake.

Inu mungathe bwanji kumakhala ndi zipembedzo ndi kumalemba malire ndi zinthu zonga izo, nkumati ndinu obadwa ndi Mulungu? Palibe chinthu choterocho. Ndi kutonza kwa—Satana. Ndiko kulondola. Koma munthu yemwe wabadwa ndi Mulungu sangakhoze kuchimwa; ndi zosatheka kuti iye achimwe.

¹³³ Penyani! Mungondilola ine nditenge mtanda uwu miniti yokha ngati iwo ungachokepo apo. Nndani anali nsembe ya tchimo? Yesu Khristu. Ife timalowa bwanji mwa Khristu? Ndani anatifera ife? Khristu. Kodi Iye anafera chiani? Machimo athu. Iye anatenga chilango changa. Nkulondola uko? Ndiyeno ndimalowa bwanji mwa Iye? Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi. Ndipo tiri mu Thupi ili, ife taphimbidwa ndi Magazi ndipo ndife afulu ku ziweruzo. Iye sangakhoze kuchimwa, chifukwa pali nsembe ya Magazi ili apo kwa iye usana ndi usiku. Aleluya! Iye sangakhoze kuchimwa. Iye alibe chikhumbo choti achimwe. Ngati iye atero—ngati iye achita chinachake cholakwika, iye samatanthauza kuti achite izo. Baibulo linati mu Ahebri mutu wa 10, “Pakuti ngati ife tichimwa mwadala ife titalandira chidziwitso cha Choonadi (ndipo Iye ndiye Choonadi), sipamakhalanso nsembe yina kwa tchimolo. Iye yemwe ankanyoza lamulo la Mose ankafa pansu pa mboni ziwiri kapena zitatu, ndi chilango chochuluka kupweteka bwanji mukuchilingalira, ngakhale woyenera, omwe awondera Magazi a Yesu Khristu pansu pa mapazi ake ndi kuwawerengera Magazi a pangano omwe iye anayeretsedwa nao ndi chinthu chosayera, nachita mosasamala ku ntchito za chisomo.”

¹³⁴ Pakuti ndi Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwira kulowa mu Thupi limodzi ndipo ndife afulu kwa tchimo, ndipo ife sitingakhoze kuchimwa. Pali chitetezero chikutiyembekezera ife. Ndipo ngati chikadalipo chikhumbo mu mtima mwanu kuti muchimwe, inu simunayambe mwabatizidwira mu Thupi limenelo, chifukwa ndinu okufa ndipo moyo wanu uli wobisidwa mwa Khristu kudzera mwa Mulungu ndi wosindikizidwa nao Mzimu Woyera. Akhristu samachimwa. Iwo amalakwitsa, koma

iwo samachimwa. Ameni! Ndicho chifukwa iwo satero, pakuti iye sangakhoze kuchimwa.

¹³⁵ Ine ndingakhoze bwanji kukhala... Ngati ine ndikanapita ndikudutsa mu mzindawu kuno, ndipo afumu a mzindawo nkuti, “Bambo Branham, ine ndikudziwa kuti inu mumapita kukawona odwala. Pali malire a liwiro. Malire a liwiro lothamanga kwambiri mu mzindawu ndi pafupi mailosi sate pa ora. Koma ine ndikukupatsani inu chilolezo kuti muzithamanga nainte ngati inu mutafuna kumatero, chifukwa ine ndiri ndi chikhulupiriro mwa inu kuti inu simungachite izo kupatula ngati inu munalu ndi kuitana koti mfulumire kapena winawake akufa kutali mu ngozi. Ndipo ine ndikukupatsani inu chilolezo, monga mfumu ya mzinda uno, kuti inu mukhoza kumathamanga pa nyali yofiira iliyonse, muzichita chirichonse chomwe inu mukuchifuna, muzingomapitirira nazo.” Angakhoze bwanji bwana wamng’ono kwambiri kundimanga ine kunja kuno pothamanga forte mailosi pa ora mu dera la sate mailosi? Iye sangathe. Ine sindingakhoze kuswa malire a liwiro lirilonse mu mzinda uno, chifukwa chiani? Ine ndiri pamwamba pa malamulo a liwiro. Ameni! Ine ndikuyembekeza inu mukuziona izo.

¹³⁶ Ndipo pamene ife tafa, ndipo Mulungu wakuzindikira kulapa kwathu, Iye wauzindikira ubatizo wathu, Iye wawazindikira Magazi a Mwana Wake yemwe, omwe mwa chikhulupiriro agwiritsidwa ntchito, Iye wakuzindikira kudzozeratu Kwake, ndipo anadziwa kuti ine ndikanadzazichita izo, ndipo wandizindikira ine mwa Khristu, wakufa... Ndipo Khristu anafa mu malo anga pamene Iye anaphedwa asanaikidwe maziko a dziko. Dzina langa linaikidwa pa Bukhu Lake monga Mkhristu. Aleluya! Khristu anafa imfa yanga. Khristu ndi Nsembe yanga. Ndipo Mulungu sakanakhoza kumawerengera tchimo kwa ine moonjezeranso. Iye wandipatsa ine Chisindikizo cha Mzimu Woyera ngati umboni kuti ine ndadutsa kuchokera ku imfa ndapita ku Moyo. Psyfuu! Izo zikukwaniritsa icho.

¹³⁷ Ndiye iwo amene ali obadwa ndi Mulungu samachita tchimo, pakuti iye sangakhoze kuchimwa. Mu Chipangano Chakale chaka chirichonse kunkakhala kukumbukiridwa kwa tchimo. Koma Khristu, ndi nsembe imodzi Iye wamupangitsa wopembedzayo akhale wangwiro kwa nthawizonse. “W—wopembedza akatsukidwa kamodzi (Ahebr 10)—wopembedza akatsukidwa kamodzi samakhalanso ndi chikumbumtima cha tchimo.” Chotero inu mukawatenga anthu awa omwe amathamanga mu tchalitchi ndi kumalumpha chokwera-ndi-chotsika mu mipata, ndi kumafuula, ndi kuyankhula ndi malirime, ndi kumachita ndendende basi ngati Mkhristu, ndi kuthamangira kunja, ndipo chaka chamawa ayenera kuti abwererenso kachiwiri, sabata yamawa. Iwo sanayambe afika paliponse pa kuyamba pomwe. Iwo akungosanzira, pakuti

Baibulo linanena kuti Mzimu Woyera umatisindikizira ife mwa Khristu mpaka tsiku la chiwombolo chathu. Aleluya! Ndi zomwe zimandipangitsa ine kukhala wotsimikiza, chifukwa Mulungu analonjeza izo.

¹³⁸ Palibenso tchimo. Funso la tchimo lakonzedwa. Ndi chifukwa chake tchimo limawoneka lonyansa kwambiri kwa Mkhristu. Ndi chifukwa chake akazi kunja kuno ovala zazifupi izi amawoneka onyansa kwambiri kwa Mkhristu. Ndi chifukwa chake makhalidwe auve, izo ndi zinthu zonyansa kwambiri, ndi chifukwa chake kusuta, kumwa, kuchita njuga, maprogramu onse awa osapimidwa pa televizioni, zinthu zonse izo zimawoneka zanyansi. Chifukwa? Inu ndinu a ku Ufumu wosiyana. Inu mwabadwira mu Ufumu wa Mulungu ndipo mwasindikizidwa ndi Mzimu Woyera mpaka tsiku la chiwombolo chanu.

¹³⁹ Iye amene wabadwa ndi Mulungu samachita tchimo ayi, pakuti iye sangakhoze kuchimwa. Mbewu ya Mulungu ili mkati mwake, ndipo iye sangakhoze kuchimwa. Utali wonse pamene Mzimu Woyera uwo uli mkati mmenemo Iwo umachotsa chikhumbo chirichonse cha tchimo kutali ndi iwe. Ameni! Iwe sungakhoze kuchimwa; palibe chikhumbo chinanso.

Ife tikhoza kutenga nthawi yaitali pa izo, koma tiyeni tifulumire. Ife sitifika powatsirizitsa iwo, ine ndikuwopa.

81. Chifukwa chiani mipingo yomwe imabatiza mu dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ndi kuleleza alaliki achikazi kuti azilalikirira, nchifukwa chiani iwo ali ndi mphamvu zochulukira kwambiri ndi ulamuliro?

¹⁴⁰ Tsopano, icho ndi chinthu cholakasa. Tsopano, ine ndikudziwa kuti ine ndikuyankhula kwa anthu omwe ati atsutsane ndi ichi, koma monga Mkhristu ine ndiyenera kuti ndinene izo. Palibe ulamuliro wa Mwamalemba mu Baibulo kwa ubatizo wa madzi mu dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Panalibe konse munthu mmodzi anayamba wabatizidwapo mu Baibulo mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Uwo ndi mwambo wa Chikatolika womwe umaphunzitsidwa mu zaka zana za sikisi.

¹⁴¹ Kukonkha sikunalipo konse mu Baibulo, kuti anthu azikonkedwa kapena kutsanuliridwa, koma kumizidwa. Ngati inu mukufuna kuti mudziwe izo, ine ndiri nawo zonse za Chigriki ndi za Chihebri pano pa izo.

¹⁴² Ndipo pa Tsiku la Pentekoste, Petro anafuna kuti munthu ayenera kuti azilapa ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha tchimo lawo. Ndipo Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera si dzina ayi. Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera... Mateyu 28:19 anati "Pitani inu chotero, kaphunzitseni mafuko onse, kukawabatizira iwo mu Dzina," osati mu maina, mu Dzina, limodzi la . . . Osati mu dzina la Atate,

dzina la Mwana, dzina la Mzimu Woyera, koma mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. *Atate* si dzina; *Mwana* si dzina; *Mzimu Woyera* si dzina. Awo ndi maudindo omwe ali a Dzina.

¹⁴³ Tsopano, masiku khumi kenako Petro anati, “Lapani, aliyense wa inu ndi kubatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu.” Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, onani momwe lapitira kutali lingaliro la autatu. . . Mukuona, iwo amayesera kuti apange amulungu atatu kuchokera pamenepo. Palibe amulungu atatu ayi. Ine ndikufuna kuti ndiwerengere izo kwa inu kuchokera mu Chigriki chapachiyambi apa. Njira yokha yomwe iwo ankabatizira mu Dzina la Yesu, ndipo Baibulo limanena mu Chigriki chapachiyambi, zinali zoti ziwapangitse iwo kuzindikira kuti Iye anali Mulungu.

¹⁴⁴ Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ndi maudindo a Mulungu mmodzi. Iye anali Atate; Iye anali Mwana; Iye ndi Mzimu Woyera. Ndi maudindo atatu kapena matumikiridwe atatu, Utate, Umwana, ndi matumikiridwe a Mzimu Woyera. Koma Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ali ndi Dzina limodzi, Ambuye Yesu Khristu.

¹⁴⁵ Munthu aliyense kuchokera pa tsiku limenelo mpakana mtsogolo anali kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo iwo anawapeza ena omwe anabatizidwa mopanda Dzina konse, ndipo Chigriki chapachiyambi chimanena pomwe pano limodzi ndi Chihebri, kuti ubatizo mu Dzina la Yesu ndi wa chikhululukiro cha machimo, zonse Chigriki ndi Chihebri. *Kuchotsa* kumatanthauza “kukhululukira,” ndithudi. Ngati ine *ndichotsa* chirichonse, ndi kuchichotsapo icho. *Kulichotsa ilo*—“kultingera kutali.”

¹⁴⁶ Koma palibe Lemba mu Baibulo. . . Ndipo Paulo mtumwi anadutsa uko ndipo anawapeza abale ena Achibaptisti, Machitidwe 19. Iwo anali kukhala ndi nthawi yopambana; iwo anali akufuula; iwo anali ndi chisangalalo chachikulu ndi zinthu zazikulu; ndipo iwo anali akulalikira, anali ndi chisangalalo mu msasa.

¹⁴⁷ Akwila ndi Prisila mu mutu wa 18 anali atadzawachezera anthu awa, Apollo; iwo anali Abaptisti. Ndipo Paulo anapita kwa iwo, ndipo iye anati, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni chanu?”

Ndipo iwo anati, “Ife sitikudziwa ngati kuli Mzimu Woyera uliwonse.”

¹⁴⁸ Iye anati, “Kodi inu munabatizidwa chotani?” Ine ndikudziwa mu King James amati “mu chiani”; mu lapachiyambi anati, “motani.” “Chiani kapena mmotani momwe inu munabatizidwira?”

¹⁴⁹ Iwo anati, “Ife tinabatizidwa ndi munthu yemweyo yemwe anamubatiza Yesu, Yohane.” Paulo anati, “Izo sizigwira ntchito

panonso. Inu muyenera kuti mubatizidwe mobwerezanso.” Ndipo pamene iwo anamva izi, iwo anabwerera mmadzi ndipo anabatizidwanso mu Dzina la Yesu Khristu. Paulo anaika manja ake pa iwo, ndipo Mzimu Woyera unadza pa iwo. Tsopano, ngati izo—ngati Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, akunena apa, ndi Ambuye Yesu Khristu, akunena apa, ine sindingakhoze kugunda zandamale zonsezo. Izo ziyenera kukhala molondola.

¹⁵⁰ Tsopano, mu Mateyu 28:19, uwo ndi mutu wotsiriza ndi ndime yotsiriza mu Mateyu. Ngati inu mukanawerenga nkhani ya chikondi, ndipo iyo nkumati, “Yohane ndi Maria anakhala mokondwa kuyambira pamenepo,” kodi Yohane ndi Maria ndi ndani? Bwerera mmbuyo koyambirira kwa bukhulo; kapeze omwe iwo ali. Kawone omwe Yohane ndi Maria anali omwe anakhala moyo wokondwa kuyambira apo. Ngati Yesu anati, “Pitani muzikabatiza mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” ndipo *Atate* si dzina, *Mwana* si dzina, ndipo *Mzimu Woyera* si dzina, ndiye kodi Iye anali kuyankhula za chiani? Kodi Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ndi ndani? Bwererani koyambirira kwa izo ndipo kawerengeni. Ine ndibwereza itatha mibadwo ya Yesu Khristu, mutu woyamba, ndime ya 18:

Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: . . . (Tsopano penyani mwatcheru kwenikweni. Chikhomo icho, ife tikuti tichitche icho *Atate*, guwa ili, *Mwana*, ichi, *Mzimu Woyera*. Tsopano, kodi Atate ake a Yesu Khristu ndi Ati? Mulungu ndiye. Kodi inu nonse mukuvomereza izo? Mulungu ndi Atate a Yesu Khristu. Uyo ndi Mulungu Atate. Uyu ndi Mulungu Mwana. Uyo ndi Mulungu Mzimu Woyera.)

Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu . . . kunali motere: . . . (Mateyu 1:18) *Pamene . . . atakwatira— amake Maria anapalidwa ubwenzi ndi Yosefe, iwo asanakhale limodzi, iye anapezeka ali ndi mwana wa . . .* [Osonkhana ati “Mzimu Woyera!”—Mkonzi.] Ine ndimaganiza Mulungu anali Atate Ake. Ine ndimaganiza Iye ankati Mulungu anali Atate Ake. Ndiye zingatheke bwanji Mulungu ndi Mzimu Woyera onsewo kukhala Atate Ake, ngati iwo ali anthu awiri osiyana, anthu awiri osiyana, umunthu, mulimonse momwe inu mukufuna kuziikira izo? Iwo ayenera kukhala Munthu yemwe yemweyo, kapena Iye anali nawo abambo ake awiri auzimu.

. . . kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: Pamene . . . Amayi ake Maria . . . anapalidwa ubwenzi ndi Yosefe, iwo asanabwere palimodzi, iye anapezeka ali ndi mwana . . . (osati wa Mulungu Atate, koma wa) . . . *Mzimu Woyera.*

Ndipo *izi zonse zinachitika, kuti zikhoze kukwaniritsidwa momwe zinanenedwera ndi Ambuye ndi mneneri, kuti,*

Taonani, namwali adzaima, ndipo adzabala mwana, . . . (Mukuona?) . . . ndipo iwo adzamatcha dzina lake Emanuele, chomwe mwa kutanthauzira chiri, Mulungu nafe.

¹⁵¹ Ndipo Dzina Lake limatchedwa chiani? Yesu. Chabwino. Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Tsopano, Atate ndi Mzimu Woyera ndi Mzimu womwe womwewo. Kodi Ghost ndi chiani? Ndi Mzimu wa Mulungu. Ndipo pamene kunatero, Iye anabwera pa ubatizo wa Yesu ndipo anadzakhala mwa Iye, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa mwa Yemwe Ine ndikukondwera kukhalamo.” Iye anabwera pansi ndipo ankakhala mwa Yesu, ndipo izo zinamupanga Iye Emanuele pa dziko lapansi. Chotero kodi Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera linali chiani? [Osonkhana akuyankha, “Yesu Khristu!”—Mkonzi.] Ndithudi ilo linali.

¹⁵² Chotero Petro anali ndi vumbulutso lomwelo. Tsopano, ife tiri nako kupenya kwathu kutaphunzitsidwira apo. Ife tikulasa pa diso la ng’ombe. Tiyeni tiwone ngati ophunzira ankagwiritsa mtundu uwo wa kawomberedwe. Nthawi iliyonse yomwe iwo ankabwera palimodzi, nthawi iliyonse ubatizo unkatshulidwa, iwo ankeyenera kuti abatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, pakuti Iye anati “Palibe Dzina lina laperekedwa pansi pa Kumwamba pakati pa anthu lomwe inu muyenera kupulumutsidwa nalo.” Ilo ndi lingaliro labodza la mdierekezi ndipo palibe Lemba nkomwe la zoterozo. Ndiko kulondola.

¹⁵³ Ndipo tsopano, ine ndikuyembekeza kuti izo sizinapweteke, koma ndi Choonadi. Mukuona? Ndi Choonadi, m’bale. Inu simungakhoze kupangitsa izo. . . Inu simungakhoze kugunda Atate, Mwana, Mzimu Woyera pa malo amodzi ndi Yesu pa ena, pamene palibe wina anayamba wabatizidwapo mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Munthu aliyense mu Baibulo anabatizidwa mu Dzina la Yesu, ndipo iwo omwe sanali atabatizidwa mwanjira imeneyo ankachita kubwera ndi kudzabatizidwa kachiwirinso iwo asanaulandire nkomwe Mzimu Woyera. Iwo akhoza kumachita ngati kuti ali nazo mphamvu zambiri. Inu muyenera kumatsatira dongosolo lopanda malire la Mulungu. Ndizo ndendende kulondola. Chabwino.

¹⁵⁴ Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ndi zolakwika. Tsopano, pa za alaliki aakazi, aliyense akudziwa kuti izo nzolakwika. Ngati inu simukudziwa mochulukuka kuposa zimenezo! Ine ndikukhumba ndikanakhala ndi nthawi kuti ndiziwerenge izo kuchokera ku Chigriki apa, zomwe icho chinanena. Anati, “Ngati akazi akufuna kuti adziwe chirichonse, asiyezi iwo

kuti akawafunse amuna awo, chifukwa ndi chamanyazi ndi zopanda chisomo kuti mkazi aziyankhula nkomwe mu mpingo.” Chigriki chimanena izo—ine ndikutanthauza, Chihebri. “Monga lamulo limanenanso asiye iwo kuti azikhala mwa chete ndi kugonjera konse kwa m’busa (mwaona?), pakuti ndi zautchimo ndi zamanyazi kuti mkazi aziyankhula mu mpingo.” Mai, aliyense ayenera kuti azidziwa izo. Ndipo tsopano. . . Chomwe njira yonse kudutsa mu Malemba, ndi Timoteo, ndi Malemba osiyana, ine ndawalemba iwo apa, ndi Choonadi. Chabwino.

¹⁵⁵ Tsopano, ndiye nchifukwa chiani iwo ali ndi mphamvu? Inu mukuti, “Kodi izo zimachita chiani?” Taona, m’bale, ndiroleni ine ndikufunsi inu, kapena mlongo, aliyense yemwe uyu ali amene akufunsa funso ili, penyani. Ine ndaiwonapo ina ya misonkhano yamphamvu kwambiri pakati pa Achimuhamedi, kukuwa, kulumpha, kutenga mpeni ndi kuwulasitsa iwo pa mtima monga chonchi, ndi kutsanulira madzi kudutsa ku nsana uko, kuyenda kudutsa pa moto ndi mapazi osaphimbidwa, china chirichonse monga choncho, kugona pa kama wa zisonga, n—ndi kutenga lupanga ndi kulilowetsa ilo nkamwa mwawo momwe ndi kumaliyendetsa ilo molicheketsa umo monga choncho—iwe umakhoza kulitenga ilo iwemwini ndi kulisolola ilo, ndipo magazi ali apo ndi china chirichonse. Musati muziyankhula za zinthu zimenezo. Mwaona? Izo si Choonadi; izo si kutsimikizira kwa chirichonse. Mukuona? Yesu anati. . . Ndiroleni ine ndiwerenge Malemba omwe ndawalemba apa kwa inu, Mateyu 7:21-23: “Ambiri adzadza kwa Ine mu tsiku limenelo. . . Si onse omwe ati, ‘Ambuye, Ambuye,’ ati adzalowe mu Ufumuwo, koma iwo omwe achita chifuniro cha Atate Anga omwe ali Kumwamba adzalowa umo. Pakuti ambiri adzadza kwa Ine mu tsiku limenelo nati, ‘Ambuye, kodi ine sindinalaliki mu Dzina Lanu. Kodi ine sindinatulutse ziwanda, ndi kunenera, ndi kuchita zinthu zina zonse izi.’ Iye adzati, ‘Chokani kwa Ine, inu ochita za kusaeruzika, Ine sindinali kukudziwani inu nkomwe.” Mukuona?

¹⁵⁶ Chotero musati. . . Taonani, Choonadi chikhoza kungobwera mwa njira imodzi yokha, m’bale. Tsopano, ine sindikunena kuti anthu omwe amawabatiza anthu mu Dzina la Yesu Khristu onsewo akupita ku gehena. Ine sindikunena chomwecho. Mulungu ndiye Woweruza; msiyeni Iye achite chirichonse chomwe Iye akuchifuna, koma palibe Malemba ololeza mu Baibulo kuti aliyense azibatizidwa mu dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.

¹⁵⁷ Paulo anamulamulira aliyense yemwe anabatizidwa mwanjira ina iliyonse mosakhala Dzina la Yesu kuti abwere ndi kudzabatizidwa mobwerezanso mu Dzina la Yesu, ndipo anati, “Ngati mngelo wochokera Kumwamba abwera ndi kudzalalikira chiphunzitso china chirichonse (Agalatiya 1:8), musiyeni iye akhale wotembereredwa.” Ndipo Paulo anati, “Monga ine

ndinanena poyamba, chomwechonso ine ndikunena mobwereza, ngati mngelo wochokera Kumwamba akanadzalalikira china chirichonse kwa inu, musiyeni iye akhale wotembereredwa.”

¹⁵⁸ Tsopano, izo sizingakhoze . . . Inu simungakhoze kupangitsa chandamale kugunda apa ndi chandamale kugunda apo. Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, nkuti, “Asiyeni iwo azipitirira, Iwo akuchita bwino!” Ndipo Dzina la Yesu, zisiyeni izo zizipitirira nkuti, Iwo akuchita bwino.” Payenera kukhala pali chinachake chomwe chiyenera kumagunda molondola. Mulungu si woyambitsa chisokonezo.

¹⁵⁹ Ndipo inu ziyendetseni izo kudutsa mu Baibulo paliponse pomwe inu mukupafuna, ndipo inu mupeza kuti uwo ndi ubatizo wabodza. Ndiye mubwerere mmbuyo ku mbiriyakale, ndi mpaka mu zaka zana za chisikisi pamene Agtobus wamkulu, ine ndikukhulupirira iye anali, yemwe anamubatiza kapena mmodzi wa . . . Ine sindinganene kuti anali Agtobus; ine ndaiwala lomwe dzina lake linali yemwe anabatizidwa . . . Ngati inu mukufuna kuti muzipeze izo mu—*Ante Nicene Fathers* usanachitike msonkhano wa Ante—Nicene, 325 a.d. iwo anali akubatizabe mu Dzina la Ambuye Yesu. Ndipo pamene mpingo wa Katolika unadza mu mphamvu iwo anatenga dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Panalibe nthawi imodzi kuchokera mmbuyomo uko, pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Uwo ndi mwambo wa Chikatolika.

¹⁶⁰ Lutera anatulukuka nazo zochulukuka za izo limodzi naye. Wesile anabweretsa zina zonse za izo, ife tikanali kupitabe kwa izo. Ndi katekisimu wa Chikatolika, yemwe amatchedwa *Faith of Our Fathers*, ine ndikukhulupirira izo ziri, pa tsamba 144, ine ndikuganiza ndi pomwe pali, iye anati—iwo anati, “Kodi wa chiprotestanti aliyense adzapulumutsidwa?” Anati, “Mwinamwake ena a iwo. Iwo amadzinenera kuti amakhala moyo mwa Baibulo, koma iwo amatengabe kuphunzitsa kwa Chikatolika.” Anati, “Baibulo, Akatolika ena, ankabatiza mu dzina la Atate—mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, koma ife tatenga mwaulemu kuchokera apo ndi kuziyika izo pa Atate, Mwana, Mzimu Woyera, ndipo achiprotestanti akuzizindikira izo.” Anati, “Mwinamwake ena a iwo adzapulumutsidwa.” Osati kuti ndi izo iwo sadzatero! Chabwino.

82. Kodi kuli oposa dziko limodzi?

¹⁶¹ Inde, pali maiko a maiko, Ahebri mutu wa 1 ndime ya 2, Ahebri mutu wa 11 ndipo ndime ya 3. Pali maiko a maiko. Mulungu analenga maiko, m-a-i-k-o, maiko.

83. Kodi kulipo kuposa kumwamba kumodzi?

¹⁶² Inde. Mu I—mu II Akorinto 12:3 Paulo anati iye anamudziwa mwamuna yemwe anatengedwera kumwamba kwachitatu. Ndi cha ku Chivumbulutso ndi zina zotero, kulipo koposa iko.

Ine ndingoyenera kuti ndifulumire, chifukwa ndi—pakali pano nthawi yadutsa yoti ine nditseke. Kodi zingakhale zabwino ngati ine nditangowerenga otsatira onse awa ndipo nkungochita (chabwino!) ndemanga?

84. Kodi khanda mwa Khristu lidzapita mu mkwatulo?

¹⁶³ Mwamtheradi, ngati iye ali khanda iye ndi wobadwa kachiwiri. Ziribe kanthu momwe iye aliri wamng’ono, iye adzapita uko mulimonse. Inu mwaona?

85. Chifukwa chiani Khristu anawonekera kwa ine pamene ndinali pafupi kuti nditenge Zopatulika?

¹⁶⁴ Chabwino, mopanda kukaika mtima wanu unali mu dongosolo ndipo inu munali mukubwera mopatulika kwa Mulungu kuti mudzachite izo; ndi chifukwa chake Iye anawonekera kwa inu. Mwaona, icho chingakhale chifukwa chokha chomwe ine ndikuchidziwa. Ine sindingakhoze kunena zoposa—kuposa zomwe izo. . . .Tiyeni tiwone.

86. Ngati ife tinapulumsidwa asanaikidwe. . . (O, o. Ife sitikufuna kuti tiime apa sichoncho ife?) Ngati ife tinapulumsidwa asanaikidwe maziko a dziko—tinali ife?

¹⁶⁵ Inde, bwana! Chivumbulutso 13:8 amanena kuti inu munapulumsidwa ndipo dzina lanu linaikidwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa dziko lisanalengedwe nkomwe. Ndipo Aefeso 1:4 ndi 5. . . .Ndiroleni ine ndingowerenga izo; izo sizitenga koma miniti yokha ndi kungoti inu muwone kuti ine sindikungo—kungobwereza izo, i—ine ndiri. . . .Chabwino, pano ife tiri; tiyeni tiwerenge izi.

Wodala akhale Mulungu ndi Atate. . . (Aefeso mutu wa 1 ndime ya 3.)

Wodala akhale Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, yemwe watidalitsa ife ndi madalitso onse auzimu mmalo a mmwambamwamba mwa Khristu Yesu:

Molingana. . . (Mvetserani!) . . .Molingana ndi momwe iye anatisankhira ife mwa iye asanaikidwe maziko a dziko, kuti ife tikhale oyera ndi opanda chilema pamaso pa Iye. . . (Monga Khristu anatifera ife, ndithudi.)

Atatikonzeratu ife ku kukhazikitsidwa kwa ana mwa Yesu Khristu kwa Iyemwini, molingana ndi chifuniro Chake chomwe chabwino.

¹⁶⁶ Tsopano, mu Bukhu la Chivumbulutso. . . .Ine ndiri nazo izo apa; ndiroleni ine ndizipeze izo mofulumira ndithu, kuti inu—inu muone kuti ine sindinali kuzikuta izo. Ine ndikufuna kuti ndizibwereze izo. Chivumbulutso 13:8, mvetserani kwa izi mofulumira basi.

Ndipo onse omwe anali kukhala pa dziko lapansi omwe maina awo—pa dziko lapansi azidzamupembedza iye, omwe maina awo sanalembedwe mu bukhu la moyo wa Mwanawankhosa wophedwa asanaikidwe maziko a dziko. (Apo ndi pamene izo zinali. Chabwino.)

87. Kodi—ife tinali mizimu ndiye?

¹⁶⁷ Ayi, ife sitinali ngakhale kanthu apo, koma mu malingaliro a Mulungu ife tinali. Ndipo Iye anayankhula izo ndipo izo zinakhalapo. Yesu anaphedwa kale. . . Ndi angati akudziwa kuti Baibulo limaphunzitsa kuti Yesu Khristu anali Mwanawankhosa yemwe anaphedwa asanaikidwe maziko a dziko. Chifukwa? Mulungu anayankhula izo, ndipo pamene Iye anayankhula izo, izo zinali monga ngati kuti zatsirizidwa. Ndipo pamene Iye anandiwona ine, Iye anakuwonani inu asanaikidwe maziko adziko, ife tinali mwachithunzi chabe mu malingaliro Ake. Ndiye pamene ife tinabwera ku dziko, ife tinali zonse mwamuna ndi mkazi, chachimuna ndi chachikazi. Iye analekanitsa mzimu wachikazi kuchokera kwa mwamuna ndipo anapanga mkazi kuchokera mwa iwo ndipo anasiya mzimu wamphongo mwa mwamuna.

¹⁶⁸ Pamene inu mumuwona mkazi akuchita ngati mwamuna, pali chinachake cholakwika. Inu mukamuwona mwamuna akuchita mwachikazi ngati mkazi, pali chinachake cholakwika.

¹⁶⁹ Ndiyeno Iye anatenga kuchokera ku mbali ya mwamuna nthiti ndipo anapanga womuthandizira kuchokera mwa iyo, ndipo iwo awiri ali mmodzi.

¹⁷⁰ Koma asanaikidwe maziko a dziko maina athu. . . Pamene Mwanawankhosa anaphedwa, maina athu anaikidwa pa Bukhu, pamene mu malingaliro ake a Mulungu Iye anatiwoneratu ife ndipo anatikonzeratu ife mwa kudziwiratu Kwake asanaikidwe maziko a dziko. O, m’bale, ngati izo sizingaupangitse mpingo kudzukapo ndi kumathamanga kudutsa mu timipita? Taganizani za izo. Inu omwe muli obadwa kachiwiri, asanaikidwe maziko a dziko, Mulungu anaika dzina lanu pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Khristu anafa ndipo anatumiza Mzimu Woyera kuno kuti udzakuitanireni inu ku Moyo Wamuyaya. Inu mwawulandira Iwo; Iye anakusindikizani inu. Inu muli mmenemo mpaka tsiku la chiwombolo chanu. Aleluya!

¹⁷¹ Kunena za kugwiritsabe. Izo sizoti, kodi ine ndikugwiritsitsabe; ndi, kodi Iye akugwiritsitsabe. Si zomwe ine ndazichita; ndi zomwe Iye anachita. Izo si, “Ine ndinasiya kusuta; ine ndinasiya bodza; ine ndinasiya kuba;” ndi kuti Iye anandifera ine. Ndipo Iye anawuchotsa mzimu wanga mwa ine ndipo ananditembenusa ine kuti ndikhale cholengedwa chatsopano.

Tsopano funso lotsatira pansu pa ilo. . . Mofulumira tsopano kuti ife tilitenge ilo.

88. Kodi pali kusi yana kotani pakati pa thupi, moyo, ndi mzimu?

¹⁷² Thupi ndi mnofu womwe inu mumayang'anapo womwe uyenera kudzavunda. Iwo unabadwa mwa chikhumbo chakugonana cha bambo ndi mayi. Ilo liyenera kuvunda. Ilo si labwino ayi. Chotero mu kubadwa kwatsopano, mu chiukitsiro pa—pamene inu mudzabweretsedwa aponso mu thupi latsopano, iyo idzakhala mphamvu ya Mulungu yakulenga yomwe iti idzayankhule monga Iye anamchitira Adamu ndipo inu mudzatulukira apo.

89. Chonde kodi mungafotokeze kudziwa kwanu koti Eva anabala Kaini kuchokera kwa mdierekezi?

¹⁷³ Ine sindinane konse izo; ine ndinati Eva anabala Kaini kuchokera kwa serpenti. Mu Genesis 4, kamodzi—ndime ya 1, momveka amalongosola kuti Adamu anamudziwa mkazi wake Eva; ndipo iye anaima, ndipo anabala Kaini, ndipo anati, “Ine ndalandira munthu kuchokera kwa Mulungu.” Mwamtheradi! Moyo wonse uyenera kuchokera kwa Mulungu. John Dillinger anachokera kwa Mulungu. Adolf Hitler anachokera kwa Mulungu. Aliyense... George—George Whitfield anachokera kwa Mulungu, ndi momwemonso Bob Ingersol. Munthu aliyense anachokera kwa Mulungu.

¹⁷⁴ Koma chomwe ine ndinanena ndi ichi: Ndipo ine ndikufuna winawake kuti angoching'amba icho. Mwaona? Baibulo linanena kuti Iye akanaike (mu Genesis 3:8). I...A... Pamene funso linafunsidwa pamene Eva anali... chinachake chinali chitachitika kwa iye, iye anakomana ndi serpenti... Tsopano serpenti sanali njoka; iye anali chirombo, chochenjera kwambiri cha chirichonse cha mu thengo. Uko kunalibe chirichonse...

¹⁷⁵ Lero sayansi ikufunafuna fupa la chinyama china chomwe chingalumikize munthu ndi nyani limodzi. Chapafupi kwambiri chomwe iwo ali nacho ndi chimpanzi. Iwo sangakhoze kulipeza fupalo. Iwo sadzatero konse, chifukwa ndi serpenti. Ilo ndi vumbulutso la Mulungu.

¹⁷⁶ Penyani! Serpenti anali—monga munthu wa mbiri yakale isanayambe, chinachake chapafupi kwa Mulungu—kapena pafupi ndi munthu. Ndipo ndi chinthu chokhacho. Ngati chinyama china chirichonse chikanafika kwa—Satana akanabwera pa icho, mbewuyo sikanati isakanizikane ndi mkazi. Inu simungakhoze kusakaniza mbewu ya munthu ndi mbewu ya mtundu uliwonse wa chinyama. Izo sizingagwire ntchito. Koma chinyama ichi chomwe chingasakanize mbewu chiri kwathunthu—icho chinatha. Mulungu anamusandutsa iye kukhala njoka. Koma kumbukirani pamene...

Anati, “Nchifukwa chiani inu mwabisala? Nchifukwa chiani inu mwaziphimba nokha ndi masamba a mkuyu?”

Ndiye iwo anayamba kupatsirana chibekete monga ankhondo amachitira. “Chabwino,” Adamu anati, “mkazi yemwe Inu munandipatsa ine wandidolola ine kuti ndidye za chipatsocho.”

¹⁷⁷ Ndipo mkaziyo anati, “Serpenti anandinyenga ine.” Tsopano, kodi *beguile* amatanthauza chiani? “I—iye wandinyenga ine.”

¹⁷⁸ Ndipo Mulungu anati, “Ine ndiika udani pakati pa mbewu yako ndi mbewu ya serpenti.” Mbewu! Serpenti anali nayo mbewu yeniyeni, ndipo iyo inabwera kudzera mwa Kaini. Kudzera mwa Kaini kunabwera anthu onse anzeru, ophunzira mpaka ku chiwonongeko cha chigumula. Ndipo kuseri kwa izo kunabwera Abele yemwe anaphedwa, ndipo Seti anautsidwa mu malo ake kuti ziimire imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro cha Yesu. Ndipo kuchokera kwa iye kunabwera anthu onyozeka, oweta nkhosa ndi ena otero, koma anthu owopa Mulungu. Ndipo Yesu anati ana a dziko lino ndi anzerupo, ochenjererapo, kuposa ana a Ufumu. Ndiko kulondola!

¹⁷⁹ Ife sitingakhoze kudzifanizitsa ndi iwo. Musati muziyesera kudziyika nokha apo kuti mukakhale monga iwo. Dzizichepetsani nokha pamaso pa Mulungu. Musati muzikhumba kuti mukhale ophunzira ndi anzeru. Muzingokhumba kumudziwa Yesu ndi kuzisiya izo zokha, pakuti apo pali mbewu ya serpenti lero. Ndipo anthu akumakhala ndi ulemerero chifukwa azasayansi, ndi amuna anzeru, ndi ophunzira, masakolala aakulu ali mu mipingo yawo. Ine kuli bwino ndikhale ndi munthu yemwe amamudziwa Mulungu kwenikweni ngati iye samadziwa ma a-b-c ake kuti akhale wa mu mpingo wanga (kulondola!) bola ngati iye ali mbewu ya Khristu.

¹⁸⁰ Mbewu ya mkazi, Mbewu ya mkazi yomwe inali Khristu. Maria anabala Khristu. Ndipo mbewu ya serpenti yomwe inali Kaini inabwera mmusi mpaka kwa Yudasi Iskarioti. Apo panali onse Yesu ndi Yudasi mu thupi apo pomwe, Mulungu ndi mdierekezi. Pa mtanda wa Kalvare apo panali anthu anai akufa. Apo panali mbala ku mbali iliyonse ya Yesu, ndipo Yudasi akudzipachika yekha pa mtengo wa mkuyu, womwe uli mtanda: “Wotembereredwa ndi iye yemwe apachikidwa pa mtengo.”

Apo panali wakuba mmodzi yemwe anati, “*Ngati* Iwe uli Mwana wa Mulungu, titsitsire ife pansi.”

¹⁸¹ Winayo anati, “Ambuye, ife tikuchita molungama, ife tikulangidwa; Inu simunachite kalikonse. Mundikumbukire ine pamene Inu muzibwera mu Ufumu Wanu.”

Yesu anati, “Lero iwe ukakhala ndi Ine mu paradiso.”

¹⁸² Apo panali—Yesu, mlaliki wa Uthenga, akulalikira pa mtanda. Apo panali Satana akubwerera ku gehena komwe, atatenge limodzi naye mbewu ya serpenti, wosakhulupirira. Apo

panali Mulungu akubwerera Kumwamba atatenga limodzi Naye wochimwa wolapa, mbewu ya mkazi. Ndithudi!

¹⁸³ Iyo sinali mbewu ya mdierekezi; iyo inali mbewu ya serpenti. Ndipo serpenti anali ndi mbewu; Baibulo limati iye anali ndi mbewu. Ndipo iyo ikadalipobe lero, mbewu ya serpenti. Mochuluka kwambiri. . .

Tsopano, inu mukhoza kundifunsa ine funso lina pa zimenezo. Ngati ife tikanangokhala ndi nthawi, ine ndiri nawo mawu onse a kwa inu, ndi. . .

90. Chonde kodi inu mungafotokeze chomwe chimatanthauza pakuti, “Sachimwa ayi” mu 1 Yohane 5:18?

Mai, tiri kumene pa izo, ine ndikukhulupirira apa. Mwinamwake izo. . . Ndapapeza; ndinatembenezira molunjika kumene pamenepo. Mwinamwake Ambuye akufuna kuti ine ndipawerenge apo. Chabwino, 1 Yohane,

Ife tikudziwa kuti aliyense yemwe anabadwa mwa Mulungu samachimwa ayi; . . .

¹⁸⁴ Ndithudi ayi! Ine ndangodutsa kumene mu izo. Iye sangakhoze kuchimwa; iye ndi wobadwa mwa Mulungu. “Samachimwa ayi,” iye sangakhoze kuchimwa, mbewu imakhalabe mkati mwake. Lemba lina lomwe inu mungati mulozereko apa lingakhale Aroma 4:8, 4 ndi 5-8 pamene Mulungu. . . Davide anayankhula, kani, zaka zinapitazo ndipo anati, “Wodala ndi munthu yemwe Mulungu sadzawerengera tchimo kwa iye (mwaona?), chifukwa iye samachimwa ayi.”

Tsopano, ife tiri nalo limodzi lina ndiyeno ndizo zonse. Tiyeni tiwone!

91. M’bale Bill, pali kusiyana kotani pakati pa ziwerewere ndi chigololo, Mateyu 19:9?

¹⁸⁵ Yesu anati mu Mateyu 19:9, “Aliyense amene amusiya mkazi wake ndi kukwatira wina, kupatula ngati chiri chifukwa cha chiwerewere, amachita chigololo.” Kusiyana kwa pakati pa chiwerewere ndi chigololo, mawuwo akhoza kugwiritsidwa ntchito mwanjira iliyonse. Koma kuti ndipangitse izo kumveka zomwe iye anali kuzikamba apopo, nkuti—mkazi yemwe sanakwatiwe sangakhoze kuchita chigololo, chifukwa iye alibe mwamuna woti amuchitire chigololo. Ndi kusayera kwa iye. Iye ayenera kuti avomereze izo kwa mwamuna wake iwo asanakwatirane ngati iye anachitapo izo. Ngati ayi ndipo mwamuna wake nadzazipeza izo mtsogolo, iye ali nawo ufulu womusiya iye, chifukwa iye anatenga lumbiro labodza. Pakuti Baibulo linati—“Zikhale bwino. . .” kapena mwambo umati. “Izi zidziwike bwino kwa inu (ine ndiri nazo izo mu wanga) ngati banja lililonse lilumikizidwa mwamtundu wina wosiyana ndi momwe Mawu a Mulungu amavomerezera, chikwati chawo si chovomerezeka. Ine ndikufuna ndipo ndikuweruzani inu nonse

motsimikiza monga muti mudzayankhire pa tsiku la chiweruzo pamene zobisika za mmitima yonse ziti zidzawululidwe, ngati aliyense wa inu akudziwa cholepheretsa chirichonse choti simuli oyenera kuti mulumikizidwe palimodzi movomerezeka, kodi inu tsopano mungazinene izo?” Ndi inu apo. Mwaona?

¹⁸⁶ Chotero chiwerewere ndi chomwe msungwana, pamene iye amakhala moyo wakusayera, icho ndi chiwerewere, chifukwa iye alibe mwamuna. Koma pamene iye akwatiwa, ndiyeno pamene iye akhala monga choncho, iye amachita chigololo molakwira mwamuna wake.

¹⁸⁷ Mkazi anabwera si kale litali, ndipo iye anati, “O, ine ndinavomereza zonse izo.” Iye anali wamanjenje, ndipo anali ndi kusokonezeka, ndipo anati, “Ine ndinavomereza zonsezo kwa Mulungu.”

¹⁸⁸ Ine ndinati, “Iwe uyenera kuti ukazivomereze izo kwa mwamuna wako. Sanali Mulungu yemwe iwe unamuchitira chigololo momulakwira; anali mwamuna wako.” Ndiko kulondola.

¹⁸⁹ Ndipo ngati mwamuna akwatira mkazi ndipo mkaziyo anakhala mwa kusayera iye asanakwatiwe naye, ndiyeno iye nkubwera kwa iye, ngati iwo akhala atakwatirana motalika kwambiri konse, ndiyeno mkaziyo nkubwera kwa mwamunayo nkuti, “Wokonedwa, ine ndikufuna kuti ndikuuze iwe chinachake. Ine ndinathamanga ndi mwamuna wina, ine sindinakuuze konse iwe,” Yesu anati iye ali nawo ufulu womusiya iye ndi kukwatira wina, chifukwa iwo sanali atakwatirana pa kuyamba pomwe, chifukwa iye monyenga anamuuzza—bodza momulakwira mwamunayo.

Tsopano, pali chinthu china apa . . . Zikomo inu.

92. Chonde tafotokozani I Yohane 5:16.

1 Yohane 5, ife tiri napo apa pomwe.

Ngati munthu aliyense amuwona m'bale akuchimwa tchimo lomwe siliri la ku imfa, iye azimufunsa, ndipo iye azimupatsa iye moyo pakuti iwo omwe amachimwa mosakhala kwa imfa. Pali tchimo laku imfa: sindikunena kuti iye azilipempherera tchimo limenelo.

¹⁹⁰ Chabwino. Ife tipite . . . Tiyeni tingozitenga izo nkuzibweretsa mmbuyo ndi kuzitenga izo mofulumira ndithu, ili ndi lotsiriza lake. Tiyeni titembenezire ku Marko, ndipo izi zifotokoza izo ndendende chomwe tchimo la ku imfa ilo liri. Pali tchimo laku imfa, ndipo iwe sumalipempherera ngakhalenso tchimo ilo. Ndi angati akudziwa kuti pali tchimo laku imfa. Iwe sumalipempherera nkomwe ilo. Tengani Marko, mutu wa 3 wa Marko. Ndipo ife tikapeza mutu wa 3 wa Marko, ndiye

mofulumira ife tikhala ndi Lemba limodzi ili tisanatseke. Tiyeni tipite ku 3 ndi 22.

Ndipo alembi omwe anabwera kuchokera ku Yerusalemu anati, Iye ali ndi Bezezebule, . . . (Iwo anamuwona Iye akuzindikira malingaliro a anthu.) . . . ndipo iwo anati, Iye ali ndi Bezezebule, ndipo ndi kalonga wa ziwanda iye akutulutsa ziwanda.

Ndipo iye anawaitanira iwo kwa iye, ndipo anati k—kwa iwo mu fanizo, Kodi Satana angamatulutse bwanji Satana? . . . (Tsopano, ngati mdierekezi angakhoze kuchiza, iye angakhoze bwanji kuchita izo?) . . . Satana angakhoze bwanji kutulutsa Satana?

. . . ngati ufumu ukhala utagawikana modzitsutsa wokha, ufumu umenewo sungakhoze kuima.

Ndipo ngati nyumba ikhala yogawanika modzitsutsa yokha, nyumba imeneyo singakhoze kuima.

Ndipo ngati I. . . Ndipo ngati Satana awuka modzitsutsa yekha, ndi kukhala wogawikana, iye sangakhoze kuima, koma ali nawo mathero.

Palibe munthu angakhoze kulowa mu nyumba ya munthu wamphamvu, ndi kulanda katundu wake, kupatula ngati iye atamumanga kaye iye—munthu wamphamvuyo; ndiyeno iye angalande katundu wakeyo.

Iye angakhoze bwanji kupita mmenemo, mu mitima iyo ndi kukapeza chiani. . . (mukuona?) kupatula ngati izo zitakhala za Mulungu?

Indetu ine ndinena kwa inu, tchimo Lonse lidzakhulukidwa kwa . . . ana a anthu, ndi kuchitira mwano mmene . . . iwo—chirichonse—yense yemwe iwo ati adzamchitire mwano:

Koma iye yemwe ati adzachitire mwano Mzimu Woyera alibe konse chikhulukikiro, koma ali mu ngozi ya chiwonongeko chamuyaya: (Ndiko kulekanitsidwa!)

Chifukwa . . . (Nchifukwa chiani Iye ananena izo?) . . . Chifukwa iwo ankati, Iye ali ndi mzimu woipa.

¹⁹¹ Kuwutcha Mzimu wa Mulungu womwe unali kuchita zozizwitsa izi mwa Khristu, iwo ankati iwo unali Mzimu wa mdierekezi umachita izo; Yesu anati ilo ndi tchimo losakhulukidwa. Ndipo ngati inu mumuwona munthu. . . Kupemphera—musati mumupempherere iye ngati iye akuchitira mwano Mzimu Woyera ndi kumayankhula motsutsa Mzimu Woyera, inu mukuletsedwa ngakhale kuti mumupempherere munthu woteroyo. Inu mukumvetsa izo? Pakuti pali tchimo laku imfa. Pali tchimo limodzi lokha. Yesu anati mtundu uliwonse

wa tchimo udzakhululukidwa kwa ana a anthu, koma kuchitira mwano Mzimu Woyera sikudzakhululukidwa konse.

¹⁹² Tsopano anthu amati, “Chabwino, kuchitira mwano Mzimu Woyera, . . .” Kodi *kuchitiramwano* ndi chiani?” Zimatanthauza “kuunena, kuunyogodola, kuuseka iwo, kuchitira mwano.” Chabwino!

¹⁹³ Kodi iwo anamchitira mwano chiyani Iye? Kunena kuti Mzimu Woyera umene unali mwa Iye, kumamupangitsa Iye kupanga ndi kumachita zinthu zomwe Iye anali kuzichita, iwo ankati, “Iye ndi wodzazidwa ndi Bezezebule, mdierekezi. Ndipo uyo ndi mdierekezi, wambwebwe mwa Iye akumamupangitsa Iye kumachita zinthu zimenezo. Kumawona zinsinsi mu mtima mwa anthu, ndi kumuza Filipino kuti Iye amadziwa komwe iye anali asanabwere ku msonkhano, ndi kutulutsa ziwanda, ndi kuchita zinthu zimenezo apo, Iye amazichita izo mwa Bezezebule, ndipo Iye ndi mdierekezi.” Ndipo Yesu ananena kuti tchimo limenelo silidzakhululukidwa konse, chotero ilo ndi tchimo losakhululukidwa loti silingapemphereredwe konse. Ilo silingakhoze konse kukhululukidwa. Mwamuna ndi mkazi yemwe angachite izo adzisindikizira okha kwamuyaya kuchoka mu Kukhalapo kwa Mulungu kwanthawi zanthawi, palibe kukhululukidwa.

Kodi inu mukumukonda Iye?

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye,
Iye anayamba kundikonda,
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

¹⁹⁴ Mvetserani, inu mwakhala abwino kwambiri, ndipo izi zakhala ziri zolimba, ndipo izo zakhala kwa nthawi yaitali. Tsopano inu mwakhala muli mu mpingo uno kuyambira 7:30, 8:30, 9:30, maora awiri ndi theka, mutakhala mu tchalitchi chotentha ichi. Inu simunachite izo kuti mungokhala pamenepo. Ndipo ine ndikuganiza magawo nainte-eyiti pa zana kapena magawo nainte-naini pa zana a osonkhana anali atakhala mu mpando momwemo kuyambira nthawi imeneyo. Ine ndikufuna kuti ndinene izi: Jeffersonville, ine ndikumverera izi; kuti wachimwa nachoka ku tsiku lake la chisomo. Ine ndikukhulupirira zimenezo. Ine ndikukhulupirira United States yense watero, koma ine ndiri nawo ena a abwenzi omvera kwambiri omwe alipo mu dziko komwe kuno mu Jeffersonville. Ine ndiri nawo anthu kuno omwe angafere pafupi nane.

¹⁹⁵ Tsopano, usiku wotentha ngati uwu, alendo omwe ali mu zipata zathu, ndiwuzeni ine komwe munthu akanati akhale kuti angokhala kuti azimumva munthu, mwinamwake, akuyankhula pa Malemba omwe iwo sakuwakhulupirira nkomwe momwe ine ndawafotokozera iwo, koma iwo ali olemekeza ndi amwaumulungu mokwanira kuti akhale ndi kumamvetsera

pa izo. Ndipo motalika inu mutakhala moyo. Pamene nyenyezi zidzasanduka fumbi, mutadzakhalapobe mwa Khristu Yesu. Mulungu atapereka chirichonse chomwe inu mukuchisowa. Iye atapereka kwa inu chokhumba cha mtima wanu. Ngati inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake ndipo mukukhulupirira kuti mapemphero anga angakuthandizeni inu, muloleni Mulungu wa Kumwamba Yemwe anamuukitsa Mwana Wake, Yesu Khristu, kuti akakhale chitetezero cha machimo athu, kuti afe mmalo mwathu, muloleni Iye Yemwe ali wamphamvuzonse, Iye Yemwe ali wopezeka ponseponse muno mu nyumba ino tsopano, Iye atapereka kwa inu chokhumba cha mtima wanu ndilo pemphero langa lodzipereka kwa wina aliyense wa inu. Ndipo mu dziko komwe dzuwa silidzawalira pa inu kachiwiri kuti likuwawuleni inu, komwe mphepo zotentha sizidzamawombako, ine ndikuyembekeza kudzakhala ndi zaka kuchulukitsa milioni ya zaka kudzakhala ndi aliyense wa inu mu Ufumu wa Mulungu ndi kudzayankhulana kwathunthu pa zinthu zamuyaya za mausiku awa ndi zinthu momwe ife takhalira limodzi. Ine ndikutanthauza izo ndi zonse zomwe ziri mkati mwanga, mtima wanga wonse. Ine ndikupemphera kuti Mulungu apereke izo kwa inu, aliyense.

¹⁹⁶ Chisomo Chake chitakhala ndi inu. Iye atakuchizani inu matenda anu. Iye atapereka kwa inu ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo ine ndikunena izi tsopano popanda kunyozetsa kulikonse, popanda. . . Ngati ine ndabweretsa kulakwira kulikonse ndi chirichonse chomwe ine ndinanena pokhudza mbewu ya serpenti, ubatizo mu Dzina la Yesu, pamene zinthu izo. . .

¹⁹⁷ Tsopano winawake akati, “M’bale Branham ndi waumodzi.” Ayi, bwana, ine si waumodzi. Ine sindimakhulupirira kuti Yesu angakhale atate wa Iye yekha. Ine ndimakhulupirira kuti Yesu anali nawo Atate, ndipo awo anali Mulungu. Koma Mulungu ankakhala ndipo anapanga kachisi mu thupi ili lotchedwa Yesu, ndipo Iye anali Emanuele, Mulungu nafe. Ndipo palibe Mulungu wina pambali pa Mulungu uyu. Iyeyo ndi Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Ndipo Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera. . . *Atate, Ambuye, Mwana, Yesu, Mzimu Woyera, Logos, Mzimu wa Mulungu. Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, Ambuye Yesu Khristu; ndi Iyeyo. Ndipo mwa Iye munali chidzalo cha Umulungu mu thupi.*

¹⁹⁸ Ndipo ine ndikukhulupirira popanda mthunzi umodzi wa kukaika, ine ndikukukondani inu, ndipo ziribe kanthu ngati inu mukhala muli obatzidwa mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera, wokonkhedwa, kutsanuliridwa, chirichonse chomwe inu mukufuna, ine ndikupemphera kwa Mulungu ndi solo yanga yonse ndi thupi kuti inu ndi ine tidzakomane mu Ufumu wa Mulungu, ndipo Mulungu adzatero, ngati ine ndikulakwitsa, sadzayang’ana pa zanga, ngati inu mukulakwitsa sadzayang’ana pa zanuzo. Koma m—mwa kukhudzidwa kwanga komwe ndi

Lemba kuti ndiyesere kupangitsa chandamale kuti chigunde kuti zikhale kuchokera ku Genesis mpaka Chivumbulutso, ine ndikukulumulirani inu kuti mukabatizidwe mobwereza kachiwiri mu Dzina la Yesu Khristu ngati inu simunachite izo.

¹⁹⁹ Ndipo ngati inu simunawulandire Mzimu Woyera, ndipo moyo wanu sukumverera kukoma, ziribe kanthu ngati inu munayankhulapo mmalirime, ngati inu munafuula, ngati inu munalumphama mmwamba-ndi-pansi, ngati inu munaikapo manja pa odwala ndipo iwo anachira, ngati inu munachitapo mitundu yonse ya zozizwitsa ndi zizindikiro, ngati inu mulibe zipatso za Mzimu za chikondi, chimwemwe, mtendere, kuvutika motalika, ubwino, kufatsa, kuleza, kupirira, chikhulupiriro ndi zinthu zonse izi mkati mwanu, ndiye ine ndikukulumulirani inu ndi kukukakamizani inu mu Dzina la Yesu Khristu kuti musalekeze kupemphera mpaka Mzimu Woyera utabwera pa inu! Ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe munayankhula mu malirime, kuchuluka kwa momwe inu munafuula, kutalika kwake momwe mwakhala muli membala wa mpingo, ngati inu mwakhala muli pano, zonse zomwe inu mwachitapo ziribe kanthu kochita ndi izo mpaka Khristu, Mzimu Woyera, atatenga malo Ake mu mtima wanu ndipo inu mutafa kwa zinthu za mdziko ndipo mukukhala mwatsopano kwa Khristu.

²⁰⁰ Mulungu akudalitseni inu ndilo pemphero langa. Tiyeni ife tiyime tsopano ku mapazi athu. O, ili ndi gulu labwino. Inu mwakhala abwino kwambiri; ine ndikungodana nazo kukusiyani inu mutaima monga chonchi.

Edith wamng'ono kumbuyo uko ali ndi tsiku lakubadwa. Edith, kodi ine ndingawerengere zako...Ine ndimupanga M'bale Neville kuti akuikireni inu izi. Ife tipeza usinkhu wa dona wamng'ono uyu womwe uli. Usinkhu wa zaka sate-eyiti. Mulungu akudalitse iwe. David, tatipatsa ife—ine ndikutanthauza, Teddy, tatipatsa ife kayimbidwe pang'ono, *Kukondwerera Tsikulakubadwa Kwa Iwe*, chabwino, ngati iwe ungate.

Tikondwerere kubadwa;
Tikondwerere kubadwa;
Tikondwerere kubadwa, Mlongo Edith;
Tikondwerere kubadwa.

Tsopano, gulu lonse ili tilumikizane limodzi, *Sitidzakalamba Konse*. Tiyeni, tonse palimodzi tsopano.

Sitidzakalamba, sitidzakalamba,
Mdziko komwe sitidzakalamba;
Sitidzakalamba, sitidzakalamba,
Mdziko komwe sitidzakalamba.

Mokoma posachedwa,
Tidzakomana mu dziko ilo;
Mokoma posachedwa,
Tidzakomana mu dziko ilo.



Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo, Bukhu Loyamba
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume One)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org